

# MAU A ULAMULIRO

Ben Howard

©2006 Ufulu wonse ndi wotetezedwa. Bukhu iri silingagulitsidwe, kapena mwa njira iliyonse kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama. Silingachulukitsidwe, kapena kutanthauziridwa mu zilankhulo zina popanda chilolezo cholembedwa kuchokera kwa:

**Ben Howard**  
**Sound Of Liberty**  
**7286 Hwy 53W**  
**Dawsonville, Georgia 30534 (USA)**

**Website Address: [www.SoundofLiberty.org](http://www.SoundofLiberty.org)**  
**Email Address: [TwoAnd@SoundofLiberty.org](mailto:TwoAnd@SoundofLiberty.org)**

*Lomasulividwa Mu Chilankhulo Cha Chichewa'*  
*Ndi*  
**Enoch Kamanula**  
**New Testament Assembly**  
**P.O. Box 64**  
**Mwanza, Malawi**

## **MAU A ULAMULIRO**

### *Mauthenga Atatu Ophatikizidwa*

#### **‘MULUNGU AMENE WALANKHULA KALE MBUYOMU- AKULANKHULANSO!’**

Uthenga wolembedwa ndi kukonzedwa kuchokera mu tepi #1070

Wolalikidwa pa March 17, 2006

Ndi M’bale Ben Howard ku

Midway, West Virginia (USA)

#### **‘UTUMIKI USANU WA KU DZIKOLAKWATHU’**

Uthenga wolembedwa ndi kukonzedwa kuchokera mu tepi #1071

Wolalikidwa pa March 18, 2006

Ndi M’bale Ben Howard ku

Midway, West Virginia (USA)

#### **‘MAU A ULAMULIRO’**

Uthenga wolembedwa ndi kukonzedwa kuchokera mu tepi #1072

Wolalikidwa pa March 19, 2006

Ndi M’bale Ben Howard ku

Glen Fork, West Virginia (USA)

*Kwa*  
*Mkwatibwi wa Khristu*  
*Bukhu ili laperekedwa*

## MULUNGU AMENE WALANKHULA KALE MBUYOMU – AKULANKHULANSO!

March 17, 2006  
Midway, West Virginia USA

Tiyeni tipemphere. *Atate Wakumwamba, Ambuye tikubwera kwa Inu pa nthawi iyi pamene tikutsegula Mau Anu apamwamba. Ndi chinthu chapamwamba kwambiri chimene chilipo mbali ino ya umuyaya ndi Mzimu wanu kudzoza pa iwo, Ambuye. Ine ndikudziwa kuti ife sitiri oyenera kutsegula Bukhu ndi kuliyang'ana, chifukwa ndi loyera. Ife tikuyang'ana za chimene chinatengera kuti ife tikhale ndi Bukhu- "Yesu anatifera ife." Kenako pali mtumiki wamkulu Paulo, iye anapereka moyo wake chifukwa cha iwo, Petro chimodzimodzinso; ndi Stefano kuponyedwa miyala mpaka imfa akuitanira pa dzina la Ambuye. Ambuye, tingachite, mochuluka motani mu nthawi ino ku Ufumu wa Mulungu? Tingachite mochuluka motani kuposa kudzipereka tokha woyera kwa inu ku ulaliki wanu? Oh, Mulungu, dalitsani Mau pamene tikuwerenga usiku uno. Ndipo mungowafulumiza kwa ife, Ambuye, pamene tikuima pano ngati chotengera chachabechabe, koma tikuyang'ana kumene kuli zonse kumene sikunalepherepo kale. Ndipo tikupempha kuti mutithandize tsopano pamene tikufunitsitsa kuwerenga ndi kulankhula Mau Anu. Mu dzina la Yesu Khristu tikupemphera. Amen.*

Ine ndikufuna kutenga lingaliro ili usiku uno, **"Mulungu amene Walankhula kale mbuyomu- Tsopano Akulankhulanso."** Ndipo ndikufuna kuyamba kuwerenga Chivumbulutso 10, Vesi loyamba. Tikuwerenga monga chonchi- *"Ndipo ndinaona Mngelo wina Wamphamvu alikutsika kumwamba,..."* Ine ndikufuna muone, Mngelo uyu Wamphamvu (ife tikuonetserani chimene iye ali potsiriza kuwerenga vesi ili) *"...wobvala mtambo:..."* Kapena wophimbika mu mtambo, chimene chikutanthauza kuti palibe amene akumuona Iye pokhapokha atakhala ndi masomphenya kuti amuone kupyolera mu mtambo, vumbulutso la chimene ali, ndi kuti ndi chiyani. Iye waphimbika mu mtambo, monga m'mene Iye anabwerera mu nthawi yoyamba. Ndi ochepa okha mwa ma milioni a wanthu amene anamuona ndi kudziwa chimene Iye anali. Pa tsiku la madyerero a Chiyuda pa Pentekosite, ndi zana limodzi kudza makumi awiri okha mu chipinda chapamwamba, patatha zaka zitatu ndi theka za kulalikira amene anaona chimene Iye anali ndipo anadziwa kuti uyu anali Mwana wa Mulungu. Kotero Iye akubwera atavala mtambo. Ndiye kenako akuti apa, kuti tizindikire ndikukhala okhutira kuti tikudziwa amene akumulankhula apa, kupitiriza vesi loyamba- *"...ndi utawaleza pa mutu Pache, ndi nkhope Yake ngati dzuwa, ndi mapazi Ache ngati mizati yamoto:"* Tsopano tikuwerenga mu chaputala, choyamba, chachiwiri, ndi chachitatu cha Chivumbulutso chimene chikuchita ndi mibado ya mpingo, ndipo zirizonse za zikhalidwe zimene zikulankhulidwa kumeneko zikuonetsera Khristu.

Ndipo akuti apa pa vesi 2- *"Ndipo anali nako m'dzanja lake kabukhu kofunyulura: ndipo anaponda nalo phazi lache lamanja pa nyanja ndi lamanzerelo pa mtunda,"* Tsopano vesi 2 ndi vesi lofunika kwambiri..., Iye kuponda phazi lake la manja pa nyanja. 'Nyanja' ndi khamu la anthu, ndipo likuyenera kuchita ndi Kum'mawa- Chapakati, kubwera Kwake koyamba. Ndipo kenako..., phazi lake lakumanzere pa mtunda. 'Mtunda' ndi kumadzulo dera lopanda anthu ochuluka. Monga anabwerera mu 1963, pamene angelo asanu ndi awiri anaonekera ku Arizona kwa mneneri wa Mulungu William Branham, ndipo chithunzi chinatengedwa cha nkhope ya Ambuye. Life Magazine inatenga nkhani yonse mu kusindikiza kwa mu July, ine ndikukhulupirira, "Kodi mtambo wodabwitsa uwu ndi chiyani umene unakwera? Angelo asanu ndi awiri anabwera ndi kulankhula kwa mneneri wa Mulungu."

Kotero Iye anaika phazi limodzi pa nyanja, phazi lina pa mtunda. Kotero ife tiri ndi mpata wa nthawi wa zaka 2, 000 pakati pa mapazi awiri amenewo a kubwera Kwake, ndipo

kabukhu kakang'ono kali kotsegula m'manja Mwake. Ndipo Paulo analankhula za inu kukhala bukhu. Iye analankhula za inu kukhala Mau. Iye analankhula nati, "Inu ndinu akalata wolembedwa wowerengedwa ndi anthu onse." Izi ziri ku Akorinto wachiwiri, chaputala 3; kumene akulankhula za inu kukhala Mau. Iye akulankhula ku vesi lachisanu ndi chimodzi, "Lemba limapha, koma Mzimu upatsa moyo." Ndipo akulankhula apo kuti ife ndife atumiki okhoza a ku Chipangano Chatsopano; osati a lemba la Mau, koma Mzimu. Kotero mu mpingo wa pachiyambi kulalikira konse kumachitika mwa kudzoza kwa Mzimu Woyera, ndipo analibe kabukhu ka m'manja koti adzidutsamo, ngati Chipangano Chatsopano. Zimayenera kubwera zatsopano kuchokera ku mpando wa chifumu wa Mulungu, pamene utumiki umene Mulungu anauika umabweretsa Mau mu mpingo; ndipo sizinali nthawi zonse kuwerenga Mau. Sizinali kutenga dikishonare ndi kutenga malemba onse palimodzi, ndi kuimirira kupereka mau kuwerenga kuchokera mu dikishonare ndi kumalumikiza malemba anu onse—loyamba, lachiwiri, ndi lachitatu. Anali amuna a Mulungu amene anaima ndi mayankho kuchokera kwa Ambuye.

Ku Akolose 1:24-25, Paulo akulankhula za 'icho chimene chiri choperewera mu chisautso cha Khristu chikupangidwa **mu thupi langa m'mene ine** ndikusautsika chifukwa cha mpingo.' Ndipo panali 'anthu' amene anali wotsogozedwa ndi Mzimu Woyera, amoyo, Mzimu wa utumiki, Mau pakati pa anthu amene akanatha kudzutsa anthu akufa. Petro ataitanidwa ku Yoppa kumene kunali mai amene anali wakufa kwa..., Baibulo silikulankhula masiku angati kapena chirichonse, koma iye anali wakufa ndipo anali atamugoneka. Iwo anatuma uthenga kwa Petro. Iye anapita, ndipo amamuonetsera Petro zovala zimene iye amasoka ndi chimene anachita, ndi m'mene analiri mai wabwino. Baibulo likuti Petro anaona kusakhulupirira kwawo. Iye anawatulutsa, ndipo anapita kumene mai wakufayo anali ndi kunena, "Dolika." Ndipo Iye anatsegula maso ake, ndipo pamene anaona kuti anali Petro iye anadzuka, ndipo Petro anamupereka iye wamoyo.

Ndi chimene kabukhu kakang'ono kali. Ndi Mau amoyo a Mulungu amene ali pano tsopano pakati pathu usiku uno kuchita chimodzimodzi chinthu chomwecho. Iye watsala pang'ono kuchita mochuluka ndipo pa zonse kusiyana ndi m'mene ife tikuganzirira. Kotero Mulungu amene analankhula kamodzi akulankhulanso. Kotero kabukhu kakang'ono kanali kotsegula pakati pa anthu. Haleluya! Khristu anali wotseguka pakati pa anthu, ndipo mpingo unali Mau; sunali Baibulo; **mpingo** unali Mau. Mau anasandulika thupi ndi kukhala pakati pathu. Chonse chimene Mulungu anali, Iye anatsanulira mwa Khristu, ndipo pamene Khristu anakwera kumwamba, chonse chimene Khristu anali Iye anachitsanulira mu mpingo. Ndipo Iye anati, "*Ntchito izi zimene Ine ndichita, zoposa izi mudzachita, chifukwa Ine ndipita kwa Atate.*" Ndipo iwo anapita kuchita ntchito zazikulu, ntchito zazikulu. Chabwino, limenelo ndiye bukhu lotseguka. Pamene Petro amayenda mu misewu ya Yerusalemu, iwo amabweretsa odwala ndipo opunduka amaikidwa mu nsewu, ndipo pamene chithunzithunzi cha Petro chimawadutsa iwo amachiritsidwa nthawi yomweyo ndi mphamvu ya Mulungu. Nkhope yake (Yesu) imawala ngati kuwala kwa dzuwa. Haleluya! Ine ndikumverera Mzimu Woyera usiku uno. Ine ndikumverera mphamvu ya Mulungu. Ine ndikumverera kagudumu pakati pa gudumu! Kotero, bukhu linali lotsegula. Moyo wa Khristu unali wotseguka ku mpingo. Palibe malire pa moyo wa Khristu usiku uno. Udzabwera kwa anthu pamene padzakhala anthu osinthika. Matupi awa a nyama adzagwa ndipo inu mudzasinthika mu kamphindi, mukutwanima kwa diso mu m'bado uno ndi m'bado umene tikukhala. Ife tiri mu nthawi yotsiriza.

Bukhu linali lotsegula. Moyo wa Khristu unali wotseguka ku mpingo wa pachiyambi. Anali Khristu mwa iwo, chiyembekezo cha ulemerero. Koma mpingo unayamba kutaya chikondi chake choyamba. Mu m'bado wa mpingo woyamba, Chivumbulutso, chaputala 2, mavesi oyamba ochepa pa Mpingo wa Efeso, iwo anataya chikondi chawo choyamba. Ndipo potsiriza unapita mu mibado ya mpingo, ndipo bukhu linasindikizidwa. Mukuona moyo

unasindikizidwira kunja ndipo iwo amakhalira mauthenga ongopulumukira; iwo anayamba ulendo wao kupita kuchipululu. Inu mukhoza kuzilumikiza ndi ana a Israeli pamene amabwera kudzatenga dziko motsogozedwa ndi Mose. Mose anatumiza azondi, khumi ndi awiri, ndipo anabwera ndikulankhula, “Ife sitingathe kutenga dziko. Ife tikuoneka ngati ziwala m’maso mwa anthuwo. Iwo ndi ziphona, ndipo ife tikuoneka ngati ziwala.” Ndipo iwo anayamba kulira ndi kupfuula ndi kunena, “Ife sitingathe kutenga dziko.” Koma tithokoze Mulungu panali awiri mwa azondi kumeneko amene anali ndi mzimu wosiyana. Yoshua ndi Kalebi anati, “Ife sikuti ndife okhoza kokha kutenga dziko, koma ndife okhoza mochuluka.” Koma ena analengeza kusakhulupirira pakati pa anthu. Iwo anati kwa Mose, “Ife sitingathe kulowamo. Iwe watibweretsa ife kuno kudzatipha ife.” Ndipo Baibulo likuti pamene anachita ichi iwo anachimwira Mulungu ponena, “Mulungu angathe?” Ndipo Mulungu anati, Bwererani ku chipululu. Mose abwezeretse iwo.” Ndipo Baibulo likuti, “Iwo anabwerera ndi kupita ku chipululu,” ndipo anali kumeneko zaka makumi anai akuzungulira ndi kumazungulira mapiri, kumadya mana amene amagwa tsiku liri lonse. Mana amene amadya amakhala ndi mphutsi tsiku loyamba likapita. Iwo analibe tirigu wa khwimbi wa dzikolo. Kenako patapita zaka makumi anai Mulungu anawatulutsa. Solomoni anazona izo; iye anati, “Ndi ndani uyu akutuluka mu chipululu atatsamira pa mapewa a wokonedwa wake?” Ine ndikukuwuzani inu, pali mpingo; ife tikutuluka mu chipululu; ife tikutsamira pa wokonedwa wathu. Ndi Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero ndi kunthawi zosatha! Ndipo tiri ndi bukhu lotseguka, kuitanidwa kotseguka kubwera kwa Iye, wonse akutopa ndi kuthodwa ndipo Iye adzakupatsani inu mpumulo. Iye adzakupatsani inu mphamvu. Iye adzakupatsani inu mtendere. Iye ndi Mulungu wobwezeretsa!

Pali zaka 2, 000 pakati pa phazi la pa nyanja ndi lina pa mtunda. Kudutsa mu zaka 2,000 zimenezo, bukhu linali losindikizidwa. Linali mu dzanja la Iye amene akhala pa mpando wa chifumu ndipo siinali lopezeka ku mpingo; kufikira Iye anabwera ndikulibwezeretsa mu tsiku lotsiriza ili ndi kuliperekanso ku mpingo ndi kunena, “Tengani ndi kudya.” Ndi nthawi imene ife tikukhalamo. Yesu Khristu ali mu mpingo lero; yemweyo amene anali mu mpingo woyamba. Palibe malire kwa Mkwatibwi. Haleluya! Zonse ndi zotheka! Chinthu chokhacho tingachite ndi kukhulupirira.

Ine ndaona nyali za galimoto zatsopano zimene ali nazo, ndipo iwo akuyenera kuona kupyola mu chifunga. Ine ndikukuuzani inu, Mulungu watipatsa ife maso atsopano amene tikhoza kuona kudutsa mu mitambo ndi kumuona Iye amene nkhope yake ikuwala ngati dzuwa. Ndi Yesu; Yesu yemweyo amene anali mu mpingo woyamba. Iye sali mosiyana mu mpingo uwu. Iye akhozabe kuchiritsa, kupulumutsa, ndi kumasula! Yesu wathu, nkhope Yake ikuwala ngati kuwala kwa dzuwa! Yemweyo dzulo, lero ndi kunthawi zosatha! Haleluya! Zonse ndi zotheka kwa iwo amene akhulupirira! Ambiri a anthu sanachigwire icho, mukuona. Iwo sanachigwire icho. Ndi kuuma kwa mitima yawo, ndi kusakhulupirira kwawo, ndi kudzikuzi pa chimene Mulungu akuchita mu nthawi ino. Yesu Khristu ndi weniweni. Iye ndi woyenera kukhalira moyo, ndipo Iye ndi chinthu chokhacho choyenera kukhalira moyo. Mphamvu ya Mulungu ndi yeniyeni. Iye ali yemweyo dzulo, lero ndi kunthawi zosatha! Popanda iye mukhoza kutaika ngati mthenga mu mphepo. Ife tikuyenera kumulora Iye kuwala. Ine ndikuganiza kuti apa ndi pamene azitumiki ambiri amapanga kulakwitsa; ndipo Mulungu andikhululukire kuti ndikulankhula motsutsa mtumiki; chifukwa icho ndi chinthu chimene sindingafune kutsutsidwa nacho kuchichita. Koma azitumiki ena amaoneka ngati kuti akufuna kuonekera ndipo akufuna kuti iwo adzimveka. Koma cholinga changa, masomphenya anga, kukhumba kwanga konse ndi kwa Ambuye Yesu Khristu amene amakhala mu mtima mwanga; Iye wandithandiza ine nthawi zambiri. Mulungu wathu ndi Mulungu amene akhoza kusuntha magudumu amene akhala ndi dzimbiri kwa nthawi yaitali.

Chivumbulutso 10:3, 4 – *“Napfuula ndi mau akuru, monga ngati mkango ubangula; ndipo pamene anapfuula mabingu asanu ndi awiri, analankhula mau awo.”* Tsopano apa

tikuyamba kufika ku chiyambi cha mibado ya mpingo. “*Ndipo pamene adalankhula mabingu asanu ndi awiriwo*, (tiri mu 96 A.D.), *ndinati ndilembe*; (taonani) *ndipo ndinamva mau...*” Osati mau a Yesu Khristu, osati mau a Mzimu Woyera, koma panali mau a ulamuliro kuchokera kwa Wamphamvuzonse- - Mulungu Wamphamvuzonse, Mzimu Wamuyaya umene uli ponseponse pa nthawi yomweyo. Panali mau a ulamuliro amene analankhula..., ndipo ndikukhulupirira kuti pali mau a ulamuliro kulankhula mu msonkhano uno. Ine ndikukhulupirira kuti tavomerezedwa kukhala pano, ndipo izo zikupanga kusiyana, mukuona. Pamene Mulungu avomereza chinachake, chimachitika. Monga dzuwa, imatuluka ndi kulowa; palibe chimene chingasinthe icho, palibe chimene chingaimike icho. Palibe nyengo ya dziko imene ingakhudze dzuwa. Iyo iri mamailosi mamilioni 93 kutali. Ife tikhoza kukhala ndi mitambo yathu, mvula yathu, mabingu, koma dzuwa lalamulidwa ndi Mulungu kuti lidzingowala. Iwo amati ilo lakhala likuchita izo kwa zaka mamiliyoni 60. Ife sitikudziwa, palibe amene akudziwa zenizeni, koma zilibe kanthu. Mulungu analamulira ilo. Iye analiyika, ndipo silingachite chirichonse koma chimene Mulungu wachiikiza kuti lichite. Kotero kuti mau a ulamuliro a Mulungu analankhula kuchokera kumwamba pamene mpingo woyamba unayamba kuchoka. Pamene iwo anayamba kutaya chikondi chawo choyamba, panali mau a ulamuliro amene anati, “Tenga bukhu tsopano ndi kulisindikiza.”

Kachiwirinso, Vesi 4- “*Ndipo pamene adalankhula mabingu asanu ndi awiriwo, ndinati ndilembe, ndipo ndinamva mau ochokera kumwamba nanena, sindikiza nacho chizindikiro zimene adalankhula mabingu asanu ndi awiriwo, ndipo usazilembe.*” Panali mau a ulamuliro kumuza Yohane kuti asindikize. Tsopano mau omwewo amene alankhula mbuyomu - akulankhulanso. Tsopano anthu ena akulankhula kuti mabingu sanalankhulebe. Ndipo zikulankhulidwa pakati pa anthu ena kuti padzakhala amuna asanu ndi awiri amene adzatuluka ndipo adzakhala mabingu asanu ndi awiri. Chabwino, ngati mabingu asanu ndi awiri sanalankhule, ndiye kuti sanasindikizidwe. **Taonani ichi bwinobwino, ndipo musachiphonye!** Ngati mabingu sanalankhule, ndiye kuti sanasindikizidwe. Chifukwa pamene mabingu analankhula, Yohane amati alembe, ndipo mau anati, “Sindikiza chizindikiro, ndipo usazilembe izo.” **Ngati iwo sanalankhule, ndiye kuti sanasindikizidwe.** Mundikhululukire chifukwa chobwerezabwerezwa, koma ine ndikumverera kutsogozedwa kuika mfundo imeneyo pang’ono. Pamene mabingu analankhula, Yohane mu 96 A.D. amati alembe zimene zinanenedwa. Koma kunalankhulidwa kuti, “Sindikiza zimene mabingu asanu ndi awiri alankhula, ndipo usazilembe.” Kotero mu 96A.D. zinasindikizidwa zonse, kotero tiyeni tione kuti ndi zisindikizo zingati zimene linasindikizidwa nazo.

“*Sindikiza nacho chizindikiro zimene adalankhula mabingu asanu ndi awiri, ndipo usazilembe.*” Sindikiza zinthu zimene mabingu asanu ndi awiri alankhula; tsopano taonani chimenecho. Kutenganso vesi 3- “Napfuula ndi mau akuru, monga ngati mkango ubangula; (Iye wakhala ali pompano kuchita izo mu mpingo woyamba, ndipo apa Iye ali mu masiku otsiriza. Izi ziri mu magawo awiri- phazi limodzi panyanja, ndi lina pa mtunda.) *Ndipo pamene anapfuula, mabingu asanu ndi awiri analankhula mau awo. Ndipo pamene adalankhula mabingu asanu ndi awiri (taonani, osati asanu ndi limodzi kapena asanu, koma asanu ndi awiri.)* Kodi pali zisindikizo zingati? Zisanu ndi ziwiri. *Ndipo pamene mabingu asanu ndi awiri analankhula mau awo, ine ndinati ndilembe; ndipo ndinamva (mau a ulamuliro) mau ochokera kumwamba...*” Mu zonse, zikuyenera kukhala mu njira imeneyo, chifukwa Mulungu analankhula. Sizingakhale mu njira ina.

Pamene mpingo unadutsa mu m’bado wa mdima, zinalembedwa mu mafanizo asanu ndi awiri a ku Mateyu, chaputala 13; kufanizira ndi ufumu wakumwamba. Poyamba inali mbewu yabwino yokhayo yomwe inalipo m’ munda. Koma pamene anthu anali kugona, Baibulo likuti, “M’dani anabwera ndikudzala; nansongole pakati pa tirigu.” Ndipo pamene anazindikira kuti panali nansongole, antchito anati, “Kodi tizule nansongoleyu?” Ndipo ulamuliro unabwera (**mau amene analamulira izo**) anati, “Ayi! Zisiyeni. Zilekeni zikulire

pamodzi kufikira nthawi ya kumapeto.” Ndipo ndi chinthu chomwecho ndi zisindikizo izi zisanu ndi ziwiri. Mau a ulamuliro analankhula kuchokera kumwamba ndi kunena, “Sindikiza zimene mabingu alankhula,” ndipo munali mu 96A.D. ndipo analamulira kuti mpingo udutse mu mibado isanu ndi iwiri ya mpingo.

Panali angelo asanu ndi awiri a uzimu, ndi nyenyezi zisanu ndi ziwiri, amithenga a pansi, nyenyezi imodzi ku m'bado wa mpingo uliwonse. Angelo asanu ndi awiri a uzimu (maso) anagwiritsa ntchito munthu wa chilengedwe (nyanga). Panali nyenyezi wamthenga ndi mngelo. Zinazungulira (kumayenda) kwa mibado isanu ndi iwiri ya mpingo, ndipo panali uthenga wopulumutsa ku m'bado uliwonse. Lutera anabwera ndi uthenga, “Olungama Adzakhala Ndi Moyo Mwa Chikhulupiriro.” Iwo anapulumuka ndi iwo. Anali mana a mu nthawi yawo. Monga ana a Israeli, pamene amadutsa mu chipululu iwo anali ndi mana, ndipo panali chinachake chimene chinapangidwa mkati mwa mana amenewo. Mvetserani apa. Panali chinachake chopangidwa mkati mwa mana amenewa pamene Mulungu amawalenga- - pakatha tsiku limodzi amakhala ndi mphutsi. Uthenga uliwonse umene umabwera..., panali chinachake chopangidwa mkati mwake chimene chimapangitsa kuti iwo upange mphutsi, ndipo oyeramtima amayenera kupita ku uthenga wina. Lutera analalikira “Olungama Adzakhala Ndi Moyo Mwa Chikhulupiriro,” koma iye analalikiranso utatu. Izo zinali mphutsi zimene zinaikidwa mu uthenga umenewo, ndipo zinapangitsa iwo kuonongeka wokha. Unapanga chipembedzo. Udakalipo lero, koma mulibe moyo wa Mulungu mwa iwo. Mulungu anapanga chinachake mkati mwa uthenga uliwonse umene unabwera kudutsa mu mibado isanu ndi iwiri ya mpingo kupangitsa iwo kuonongeka wokha, chifukwa panali uthenga wina kubwera. Ngakhale wamthenga wa m'bado wa chisanu ndi chiwiri, M'bale William Branham anabwera ndi kulalikirira Mau a Mulungu, ndipo anaikamo zina zimene zikanapanga iwo kuonongeka okha, kuti ife tikathe kutenga sitepe ina. Ife, ngati ana sitimakonda kutenga sitepe. Ife sitimakonda ululu umene timaumva. Koma M'bale Branham amalankhulapo zina ngati izi, “Mau samabwera kwa wina aliyense koma mneneri” ndipo “Mulungu amakhala ndi mneneri m'modzi pa nthawi imodzi.” Chonde tandionetsani ine ku Chipangano Chatsopano kumene mungapeze izo? Kotero, pali mamilioni a otsatira ake amene akulalikira kuti Mau samabwera kwa wina aliyense koma mneneri, ndipo akuti Mulungu ali ndi munthu m'modzi pa nthawi imodzi. Chabwino, nanga bwanji atumwi khumi ndi awiri ku Israeli? Nanga bwanji Paulo ndi utumiki kumeneko? Ndipo kunali Agabo, Yuda, ndi Sila- aneneri atatu a ku Chipangano Chatsopano ku bukhu la Machitidwe. Kotero pakubwera uthenga kudzionga wokha kuti upereke malo kwa wina, chifukwa Mulungu akuchotsa malire. Anali mana ndipo panali chinachake mwa iwo kupangitsa iwo kukhala ndi mphutsi ndi kudzionga wokha. Inu ndi ine tikuyenera kudzuka pa mapazi athu ndikupitirira, chifukwa ngati inu simungapitirire inu mudzionga nokha ndi iwo. Inu mukhala chipembedzo chopanda dzina ndikukhala oyipa monga ena a iwo, chifukwa mana amenewo anachita monga ena onse ndi kudzionga. Mulungu anaziikiza izo monga choncho. Koma padzakhala gulu la nkondo limene lidzadzuka pa mapazi awo ndi kunena, “Ine ndimawerenga ku Aefeso, chaputala 4; kumene pofikitsa oyeramtima ku ungwiro Mulungu anapereka, “atumwi, aneneri, alaliki, abusa, ndi aphunzitsi.” Kotero anaperekanso mphatso khumi ndi zinai kudalitsa ndi kumangirira thupi, ndipo Iye amaziika izo mu mpingo ndipo mpingo umangoyendabe! Haleluya.

Ine ndikuyembekezera kuti inu tsopano mukuona pamene mabingu ndi zisindikizo zanu ziri. Tsopano tayang'anani pamene mau a ulamuliro akulankhula. Iye akuti, “Sindikiza mabingu ndi zisindikizo zisanu ndi ziwiri.” Kotero chonde mundiuze m'mene zingakhalire kuti mabingu asanu ndi awiri sanalankhule. Ngati iwo sanatero, ndiye kuti ife tiri ndi zaka zikwi ziwiri kapena zitatu kutsogoloku ya mibado ya mpingo, ngati iwo sanalankhule. Chifukwa pamene iwo alankhula, akuyenera kusindikizidwa. Musaphonye izi tsopano! Pamene alankhula, akuyenera kusindikizidwa. Ndipo iwo anasindikizidwa mu 96 A.D.

pamene mau a ulamuliro a Mulungu analankhula; koma zinachitika kudutsa mu mibado isanu ndi iwiri ya mpingo ndi amithenga asanu ndi awiri.

Kotero, mu m'bado wotsiriza wa mpingo uwu, M'bale Branham anali ku Arizona, angelo asanu ndi aiwri anabwera amene anatumizidwa kuchokera pamaso pa Mulungu. Iye anabwerera ku Jeffersonville, Indiana ndi kulalikira zisindikizo zisanu ndi ziwiri. Uko kunali kumasula mofanana chimene mabingu amenewo (angelo auzimu) ananena mu tsiku la Yohane. Usiku uliwonse m'modzi mwa angelo a uzimu amabwera ndi kudzaulura chimene chinali chisindikizo. Ndipo tsopano chadziwika, tsamba limenelo la mbiri latembenuzidwa. Tsopano ife tikupita ku Chipangano Chatsopano, ndipo chiri chonse chimene chinalonjezedwa ku Chipangano Chatsopano chalozera ife. Machiritso, madalitso, mphamvu, chimwemwe, chikondi – zonse ndi zathu. Zinthu izi ndi zenizeni, ndi zabwino, ndi zokoma, ndipo ndi zapamwamba. Ndi zimene tikukhalira moyo. Ichi ndi cholinga changa. Ngati inu muli ndi moyo popanda cholinga, ndiye kuti moyo wanu suli wabwino. Koma ngati muli ndi cholinga, ndiye inu muli ndi chimwemwe, inu mukudya uchi umenewu kuchokera ku kabukhu kakang'ono kamene kamakupatsani inu cholinga. Kamakupatsani inu mphamvu. Kamakupatsani inu masomphenya. Kamakupatsani inu 'pita iwe.' Kamapanga moyo kukhala woyenera kuukhala. Kamapanga zonse kukhala zabwino.

Dziko lonse lapansi mphungu zazing'ono zikukweza mitu yawo kumva mau. Alemekizeke Mulungu, pali liu limene likupita! Ndipo pali anthu kudutsa mu internet pa dziko lonse, kumva liu, kudzuka ku vumbulutso, kubwera ku Mau.

Tsopano limodzi la masiku amenewa, ngati Ambuye sabwera msanga, ine sindikukaika ndidzachoka mu dziko njira iyi ya moyo. Ine sindikunena kuti ndikupita mu masabata awiri, zaka ziwiri, kapena chinachake; ine sindikudziwa. Koma pamene ine ndiri pano, ine ndiri ndi cholinga; ndiri ndi chochita; ndiri ndi china choti ndichite. *Mungondilimbikitsa Ambuye. Kapolo wanu kudzagwira ntchito. Tilimbikitseni ife, ndipo Ambuye, mutithandize ife tonse kunena, "Tiyeni tipite ndi kukatenga dzikolo. Tiyeni tikhale mu mpingo umene Mulungu akhoza kuumwetulira ndi kuyang'ana pa iwo ndikunena, "Awa ndi anga. Awa ndi anga. Awa ndi amene ali mu bukhu la chikumbutso limene ndalipanga." Amen.* Ndipo ife sitimanena, "Chabwino, ine nditsatira mlaliki uyu, ndipo ine sindidzamvera chirichonse aliyense adzalankhula." Chabwino, ife tikuyenera kutsatira mlaliki, chifukwa Mulungu anawaika iwo m'menemo kuti atitsogolere ife. Koma lorani mlalikiyo akhale kumbuyo. Lorani iye akhale mthunzi, koma lorani Khristu ayimirire pamenepo ndikulora nkhope yake kuwala. Ife tidzayenda ndi chimenecho. Ngati pali mtumwi, chimene ndikukhulupirira kuti alipo, zidzadziwika zokha, ndipo sizidzakhala kuti wina wake adzaomba lipenga kunena, "Ine ndine mtumwi; ine ndiri ichi, ndi zina zotero." Udzakhala uthenga umene udzapita ndipo udzapita ndi kutenga anthu. Ndipo anthu amene adzamva iwo adzadziwa kuti pali chinachake pa liu limenelo, kuti 'likumveka bwino kwa ine.' Mulungu kuika chinachake palimodzi apa. Iye akubweretsa chinachake palimodzi chimene munthu sangathe kubweretsa palimodzi. Iye akubweretsa anthu palimodzi kuchokera ku dziko lonse lapansi.

Ine ndikufuna inu muone, mau analankhula ndi kulamulira chinachake; ndipo kunali kulamulira ndi kusindikiza chimene mabingu analankhula zaka zikwi ziwiri zapitazo. Tatangani bukhu losindikizidwa ku Chivumbulutso, chaputala 6. Limadzitsegula lokha, ndipo zinatenga zaka 2,000 kuchita zimenezo. Choyamba wokwera kavalo woyera anapita, ndiye wotsutsa khristu woyamba kubwera pamenepo kudzionetsera yekha. Kenako kavalo wofiira-kuyesera kupha oyeramtima. Kenako kavalo wakuda - amene anapititsa dziko mu m'bado wa m'dima, ndi zina zotero kungsi wa mzere mpakana lero tabwereramonso. Ife tiri kumudzi! Ndi chifukwa Mkwatibwi akunena, "Ndiwonetsereni ine Khristu! Ndiwonetsereni ine moyo wina! Ndiwonetsereni ine nkhope imeneyo yowala ngati dzuwa!"

Mavesi 5-6- "Ndipo mngelo amene ndinamuona alikuimirira pa nyanja ndi pa mtunda (taonani malo aliwonse- panyanja ndi pamtunda- Iye sakufuna ife tiphonye zimenezo)

*anakweza dzanja lake lamanja kuloza kumwamba, nalumbira kutchula Iye amene ali ndi moyo kunthawi za nthawi, amene analenga...*” Tsopano ine ndikufuna inu muone- Osati Yesu, osati Mzimu Woyera- iwo onse ali mwa Mulungu m’modzi, mukuona. Koma Mulungu Mwiniyekha Wamphamvuzonse, Mzimu Wamuyaya, wopezeka paliponse nthawi iliyonse, Iye analankhula, ndipo kenako Mngelo Wamkulu akukweza dzanja lake ndi kulumbira pa Iye. Tsopano pamene Mulungu anapanga pangano ndi Abraham, kodi Iye analumbira pa ndani? Iye analumbira pa Iye yekha, chifukwa palibe aliyense wamkulu. Pamene Yesu anali pano Iye anati, “Atate Wanga ndi wamkulu kuposa ine. Iye ndi wamkulu kuposa wonse.” Kotero apa, Khristu ngati Mngelo Wamkulu mu gawo iri, ntchito ya udindo apa, anakweza dzanja lake kumwamba ndikulumbira pa Iye amene akhala ndi moyo ku nthawi za nthawi. “...amene analenga m’mwamba ndi zinthu ziri momwemo, ndi dziko lapansi ndi zinthu ziri momwemo, ndi nyanja ndi zinthu ziri momwemo kuti sipadzakhalanso nthawi:” Kutanthawuza kuti m’bado umenewo wafika ku mapeto. Mibado ya mpingo yafika kumapeto, pamene Mkwatibwi watulutsidwa kukakomana ndi Khristu, Mkwati wake. Ndi chimene vesi ili likutionetsera ife; taonani pamene tikuliwerenga ilo. Vesi 7 – “*Komatu m’masiku a mau a mngelo wachisanu ndi chiwiri m’mene iye adzayamba kuomba, pamenepo padzatsirizika chinsinsi cha Mulungu,* (osati zinsinsi; chinsinsi chimodzi kuchita ndi mibado ya mpingo) *monga analalikira kwa akapolo ake aneneri.*”

Mwa kulankhula kwina, chimene ndikulankhula ndi ichi, pamene Mngelo Wamkulu (Khristu) atsika, zimenezo zikutsiriza nyengo ya nthawi iyi. Inde, izo zikutsiriza nyengo ya nthawi imene bukhu likusindikizidwa ndi kutsegulidwa, tsopano poti angelo asanu ndi awiri amenewo auzimu abwera ndi kutsegula kwa ife zimene zinasindikizidwa mu 96 A.D. Tsopano inu mutayamba ndi vesi 8-11 la Chivumbulutso, chaputala 10, inu mudzapeza kuti mau omwewo a ulamuliro amene analankhula poyambirira kwa Yohane mu mavesi 3-7, akulamulira chinachake. Ndipo zidzakhala, zidzatero, ndipo ziri choncho. Ine ndibwino ndingozitenga ine ndekha..., koma ndikuuzani inu, padakali vinyo mu botolo la vinyo. Vinyo watsopano, akamuika mu zikopa zakale, zimaphulika. Koma Mulungu ali ndi vinyo watsopano amene akuyenera kulowa mu zikopa zatsopano. Inu mukaika vinyo watsopano mu zikopa zakale zidzangolekanitsa izo; pakuyenera kukhala kutakasuka, chifukwa vinyo ameneyo amagwira ntchito ndipo amayendayenda, ndi zina zonse za izo.

Ife timakhala tikuimba nyimbo pamene ndinali mwana mu gulu la mpingo wa Holiness. Mbuyomo masiku amenewo ine ndimakonda mpingo umenewo wa Holiness chifukwa iwo anandiphunzitsa ine, kundisunga ine, ndi kundithandiza ine. Koma chinthu chokhacho ine ndimachita pamene ndimalalikira kunali kutumpha, kunjanja, kukuwa ndi kumenyetsa mapazi anga pamodzi, ndi kunena, “Mulungu kodi siwabwino?” Kenako ine ndimatha kuthamanga uko ndi uku pamalopo, ndi kuwapanga anthu kupfuula. Kotero usiku wina ine ndinachita zimenezo, ndipo anthu onse amasangalala ndi kumapfuula. Patsogolo pake, ine ndinamufunsa m’busa wanga, “Ine ndinazichita motani usiku uno?” Ine ndimayembekezera kuti iye anena, “Mzanga, iwe wagwira ntchito yabwino.” Iye anati, “Chabwino, iwe unachita phokoso lambiri, koma chenicheni chochepa.” Zinali ngati kubaya baluni ndi msingano. Kotero ine ndinaganiza, “Ine ndikuyenera kuyamba kuwerenga.”

Ine ndikukhulupirira padakali chenicheni kwa ife, sichoncho? Ine ndikukhulupirira kuti Iye amene waima, amene nkhope yake ikuwala ngati dzuwa, imene inawala ngati dzuwa ku mpingo woyamba, nkhope Yake ikuwalabe ngati dzuwa.

Mulungu akudalitseni usiku uno. Ine ndimakukondani ndi kunyadira inu. Pamene ndiri pano masiku ochepa otsatirawa, ine ndiri pano kukhala kapolo wa Mulungu mu njira iriyonse ndingakhalire thandizo kwa wina aliyense. Ine ndine kapolo wake, ndipo ngati ndiri kapolo wake, ndine kapolo wanu. Amen.

## UTUMIKI USANU WA KU DZIKOLAKWATHU

March 18, 2006  
Midway, West Virginia USA

Moni kwa aliyense wa inu, ndiye mu gawo iri la uthenga ife tikhala tikuchita ndi chinachake cha padera, chimene chalonjezedwa kwa anthu a Mulungu a mu nthawi yotsiriza. Ndi chokhudza kutulukanso mu chipululu kachiwiri, komanso m'mene ana a Israeli anakhalira ndi lonjezo lotenga dzikolo, ngakhale kuti iwo amangozungulira mu chipululu. Mulungu anawauza zimene zinali ku dzikolo ndipo iwo analandilako ngakhale zina mwa zipatso za dziko lapamwambalo la Kenani. Ena mwa azondi anapitako ndi kukabweretsa magulu a zipatso zimene zinali zazikuluzikulu, ndipo zinatengera amuna awiri kuzibweretsa. Yoshua ndi Kalebi anati, "Ndi dziko lapamwamba, ndi dziko lalikulu, ndipo izi ndi m'mene ziriri kumeneko." Koma azondi ena amene anapita limodzi ndi Yoshua ndi Kalebi anafalitsa kusakhulupirira pakati pa anthu; ndipo chifukwa cha ichi, iwo amayenera kubwerera ku chipululu kwa zaka zina makumi anai., koma amadziwa chimene chinali ku dzikolo iwo asanabwerere ku chipululu. Inde Israeli amadziwa kuti kuli dziko lalikulu kwinakwake, ndipo lonjezo la Mulungu linali lake kuti atenge dzikolo, ndipo mwa vumbulutso ambiri a ife talowa kale mu ilo..., monga Israeli analowa mu dziko la Kenani.

Tsopano pamene ife tabwera pakati panu masiku awa atatu kuchita kampeni ya Mau a Mulungu; ife tikubwera modzipereka kwa azibusa amene ife timagwira nawo ntchito pamodzi. Ife sitikubwera kudzanena kuti ife timadziwa zonse kapena china chake ngati choncho. Koma tikubwera kudzaimirira Ambuye Yesu Khristu, ndipo iye ayika zinthu zimene ife tikuzisowa, ndipo zikhala zabwino ndipo zikhala zinazake zimene tikhoza kuona Mulungu mwa izo. Pali mutu umodzi wa mpingo ndipo ndi Khristu. Ife tonse ndife akapolo ake ndipo Mulungu amatiika ife pa malo athu, monga aliyense ali nawo maitanidwe, ndipo ife tikuyenera kukhalabe mu maitanidwe amene taitanidwira ku ntchito Yake, koma tikuyenera kukula mu maitanidwe amenewo. Ife tikuyenera kukula mu chidziwitso ndi chisomo cha Mulungu.

Pamene tikupita, mu tsiku iri lotsiriza, pali lonjezo ndipo limatiuza ife cheni cheni mu Mau a Mulungu chimene chidzakhale kusuntha kotsiriza kwa Mulungu, ndi zaka zotsiriza zimene mpingo udzakhale pa dziko. Zakhala ziri choncho kudutsa mu mibado yonse, ife tagwira ntchito zaka zambiri pansu pa uthenga opulumukirapo, kuchita chimene tikanachita kuti tikhale ndikuti tipulumuke. Panali cholinga pa icho, chifukwa Mtengo wa Moyo unali utasindikizidwa. Sikuti unali utasindikidwa kokha, koma unali kumwamba, ndipo unali mu dzanja la Mngelo Wamkulu, ndipo siunali wopezeka kufikira m'masiku otsiriza, mpakana zisindikizo zitatsegulidwa ndi Mwanawankhosa kumwamba, kubweretsedwa pa dziko ndi kuululidwa kwa wanthenga wa m'bado wa chisanu ndi chiwiri (William Branham) mwa angelo auzimu asanu ndi awiri amene anabwera ndi kukumana ndi iye ku Arizona. Iye anati usiku uliwonse m'modzi mwa angelo amenewa amabwera ndi kudzaulura chimene chisindikizo chirichonse chinali. Pamene chimenecho chinachitika, ndipo zisindikizo zonse zinatsegulidwa, ndiye kenako kabukhu kamene kali mudzanja la Mngelo Wamkulu ndikotsegula. Ndipo Mngelo Wamkulu akubwera ku dziko ndi bukhu lotsegula, ndipo pa nthawi iyi mau aulamuliro kuchokera kwa Wamphamvuzonse akulankhula. Tsopano tiri nawo ufulu kupita kwa Khristu ndi kunena kwa Iye, "Ndipatseni kabukhu kakang'ono." Bukhulo ndi lotsegula, liri pa dziko.

Mneneri William Branham anabwera ndikubweretsa uthenga. Inde, uthenga wake unayamba magawo akubwera kwa chinthu chapamwamba ichi chimene chiri pakati pathu. Chifukwa Mau akuti, "Kuti Ambuye Mwiniyekha adzatsika kuchokera kumwamba ndi Mfuu, ndi mau a Mngelo Wamkulu, ndi lipenga la Mulungu." Kumbukirani apa kuti uthenga wa

M'bale Branham, palimodzi ndi uthenga wa M'bale Raymond Jackson ndi gawo lofunika kwambiri pa gawo lililonse. Mapeto a zonsezi ndi **“lipenga la Mulungu,”** limene ndi nthawi imene padzakhala mau a ulamuliro amene inu mukhoza kungomva mu Mzimu, kukuuzani inu kupita kukatenga kabukhu kakang'ono mu dzanja la Mngelo. Ndipo inu mudzakhala mukulankhula, “Mulungu, ndipangeni ine kukhumba kumva ndi kumvera chimene Mzimu ukunena, chimene mau a Wamphamvu zonse akunena. Monga tikudziwa tsopano kuti pakhala pali mau a ulamuliro akunena, “Pita kwa Mngelo Wamkulu ndikukatenga bukhu.” Ndipo izi zichitika kwenikweni kumapeto kwa nthawi. Bukhu likangotengedwa, ife tipita ku chimene Paulo anachiika ndi kuti chidzakhala pano. Iye anatipatsa ife Mau ndi uthenga ndi kutipatsa ife kachitidwe, ku utumiki choyamba- ku ungwiro wa oyeramtima, ndipo kenako zimafalikira kupita ku thupi lonse. Pali mphatso zisanu zotumikira ku utumiki, ndipo zapatsidwa kwa amuna oitanidwa ndi Mulungu. Komanso pali mphatso zisanu ndi zinai ndi zipatso za mzimu pa thupi, ndipo zonsezi ziri za tonse a ife –amuna ndi akazi.

Mulungu anaika utumiki iye asanamutenge Paulo pa dziko. Paulo analankhula ndi akulu akulu aku Efeso ndi kuwauza kuti, “Inetu ndikuyenera kuchoka. Nkhondo yanga yatha. Yatha. Koma pali amuna pakati panu tsopano, amene ine ndikangochoka, iwo adzadzuka ndikudzitengera okha ophunzira.” Iye analankhula ndikuzifotokoza momveka bwino kuti nthawi yake yatha. Iye anapita ku Yerusalemu ndipo anamutengera ku ndende. Koma mu 64 A.D., Mulungu asanamulore iye kuchotsedwa kwathunthu padziko ndikupita ku mudzi ku Ulemerero, iye anatilemba ife bukhu; limatchedwa Bukhu la Aefeso. Ndipo mu chaputala chachinai cha bukhu limenelo, iye anatifotokoza za utumiki umene Mulungu adzagwiritse ntchito kufikitsa Mkwatibwi ku ungwiro. Ndi utumiki uwu, Mkwatibwi adzafika ku malo amene iye sadzagwedezeka uku ndi uku ndi mphepo iriyonse ya chiphunzitsa ndi tsenga la anthu. Iye anatiuza ife za utumiki umene udzakhala pa dziko pa nthawi imene ife tidzafika ku ungwiro wa thupi la Khristu, ndipo mamembala a thupilo adzayamba kumangirirana wina ndi mzache mu chikondi, ndipo ife timakula mu uthunthu wa munthu Khristu Yesu.

Tsopano zinalembedwa ndi kusiyidwa mu Mau kwa ife kuti pamene nthawiyo ifika, ndiye kenako tikhoza kukhala nako, mu **malemba olembedwa**, kachitidwe, Mau, “utumiki” – kuti ife tisazungulirensa mu chipululu, ndi kuti ife (utumiki) tikhoza kudziwa, ndi kuziyika poyera pamaso pa anthu mapo amene aikidwa kwa ife kuti titsatire ku ungwiro otsiriza. Chifukwa Mulungu akutiitana ife kuchita chinachake chimene sanaitanirepo m'bado wina uliwonse kuchichita. Iye akutiitana ife kupita mwakuya ndi patsogolo mu Mau, ndi makamaka kutenga **zonse** zimene Iye waziika kwa Mkwatibwi mu nthawi yotsiriza, kuti iye akakwatulidwe. Utumiki walembedwa ndipo ife tautidwa za iwo ku bukhu la Aefeso.

Tsopano ife tadutsa mu magawo a zisindikizo, (kusindikizidwa kwa bukhu, ndi kutsegulidwa kwa bukhu). Mulungu analankhula mu masiku a Yohane ndi kumulamulira iye kusindikiza bukhu ndi kuti asalembe; chifukwa zimayenera kudutsa mu nthawi yaitali iyi. Koma tsopano nthawi yayitaliyo yatha, monga m'mene nthawi yongozungulira mu chipululu ya ana a Israeli inathera. Koma kumbukirani kuti asanalowe mu chipululu, Mose anali atapatsidwa kale malangizo okhudza dzikolo. Ndipo panali mamuna wina otchedwa Kalebi amene anaima phewa ndi phewa ndi Yoshua, ndipo Mose anali atamulonjeza iye phiri kumeneko- (“Pamene mudzalowa mu dzikolo, phiri iri lidzakhala lako.”) Koteru pamene iwo analowa mu dzikolo, Kalebi anapita kwa Yoshua, amene anali mkulu wa gulu la nkhondo la Israeli, ndipo anati (mongotchula), “Ndipatseni tsopano phiri limene kapolo wa Ambuye, Mose, anandilonjeza ine.” Ndipo Yoshua anamuchenjeza, “Kuli ziphona ku phiri limenelo, Kalebi, ndipo iwe wakula. Mwina iwe ukhoza kukhala okondwa kutenga dera lina kuno ku chigwa, kapena dera lina kwinkwaka kumene kukhoza kukhala kosavuta kutenga.” Pamene Yoshua amalankhula ndi Kalebi kumeneko...., Kalebi anali ndi mzimu wina. (Mongotchula) Iye anati, Ine sindikudandaula ndi ziphona; mungondipatsa ine phirilo limene Ambuye Mulungu adanena kupyolera mwa Mose kuti ndidzakhala nalo ndipo ndidzalisamalira.”

Ine ndikulankhula zimenezi kuti ndilankhule chonchi- iwo anali ndi chidziwitso cha izo; ngakhale kuti anali akungomazungulira ku chipululu. Iwo amadziwa kuti kunali dziko kwinkwake kumene iwo amapitako. Ife tinali nacho chidziwitso cha izi, ngakhale kuti sitinali kwathunthu titatenga ilo mu gawo lonse la Mau. Inu mukuyenera kudziwa lonjezo limene liri la inu inu musanafike potenga ndi kufunsa lonjezolo. Zaikidwa bwino ndipo momveka za utumiki umene Mulungu akugwiritsa ntchito kufikitsa oyerantima ku ungiro. Izi zisanachitike, iwo anali nazo njira zosiyanasiyana. Kudutsa mu mibado ya mpingo kunali munthu m' modzi (wamthenga nyenyezi) ku m' bado uliwonse. Mulungu amagwiritsa ntchito wamthenga ndipo ena onse amatsatira. Koma ife timabwera ku chinachake ndipo tsopano tafikako! Ndipo ndiri pano kukuuzani kuti ndi nthawi yoti titenge dzikolo. Ndi nthawi yoti tifunse za chimene Mulungu watipatsa – “Chimenecho ndi kutenga dzikolo.”

Mulungu analankhula ndi Yoshua za kutenga dzikolo, ndipo Iye anati, “Taona khala wolimbika. Khala wamphamvu, ndipo khala wolimbika kwambiri. Ambuye ali ndi iwe.” Ndipo pamene Yoshua anayamba kudutsa mu dzikolo, iye amayenera kuwauza anthuwo kuti adziwe zimenezo..., “Ambuye watipatsa ife dzikolo.” Iye anawalora anthuwo kudziwa kuti panali lonjezano ndipo inali nthawi yofunsa lonjezanolo. Ndipo pamene iwo anayamba kuoloka Yordano kumeneko, chinthu choyamba chimene iwo anawona chinali munthu ali ndi lupanga mu dzanja lake. Yoshua anayenda kumutsata iye ndi kulankhula “Kodi uli m' modzi wa ife kapena adani athu?” Ndipo Iye anati, “Ine ndine mkulu wa gulu la nkondo la Ambuye wa makamu; Ine ndipita nanu.” Iwo anali nacho chirimbikitso. Iwo amadziwa kuti samayenera kumangozungulira. Iwo samayenera kulankhula, “Kodi izi zikhoza kukhala zenizeni?” kapena “Kodi izi zingakhale zolondora?” kapena “Kodi iyi ndi nthawi yake?”

Ku bukhu la Nehemia, pamene Mulungu anawabweretsa ena mwa ana a Israeli kuti adzamanenso mzinda umene unali utagwetsedwa ndi Nebukadinezara, ambiri a iwo anayamba kumamanga nyumba zawo, anayamba kumachita zinthu zawo ndikumayamba kulankhula kuti, “Sinthawi yomanga nyumba ya Mulungu.” Koma Mulungu anali ndi liu pakati pawo ndi kuwauza iwo, “Ndi nthawi yomanga.” Ndipo pamene anayamba kumanga, panali otsutsa ambiri, chifukwa chinali chaching'ono, chifukwa ochepa okha ndi amene anapita kukamanga chimpana chachikululo cha kachisi. Ena mwa iwo amaseka ndikumalankhula, “Chimene akumanga anthu awa ngati nkhandwe atagunda khomalo lidzagwa.” Tumizani nkhandwezo; ife tipitiriza kumanga! Mulungu alemekezeke! Mukuona, Mulungu walamulira chinachake. Pali liu limene lalamulira chinachake mibado ya mpingo itatha, zisindikizo zitatha, titatha kutuluka mu chipululu, ndiye kenako ife tinadutsa kuchokera ku Chivumbulutso 10:7 kupita ku Chivumbulutso 10:8 ndipo tiri mu dziko latsopano. Ndi mau omwewo amene analankhula kwa Yohane mu 96 A.D, ndikumuuza iye kuti asindikize bukhu. Ndi liu lomwelo limene lidanena kwa Yohane mu 96 A.D, mu masiku pamene mngelo wachisanu ndi chiwiri adzaomba, “chinsinsi ichi” chidzatsirizika. Kutsirizika uku kwa “**chinsinsi ichi**” kunali kutsegulidwa kwa zisindikizo (chimene ndi vumbulutso la mabingu asanu ndi awiri) chimene chinali chosindikizidwa kuyambira m' masiku a Yohane pa chisumbu cha Patmo mu 96 A.D., koma chinamasulidwa mu tsiku lathu mu 1963.

Tsopano tiyeni tibwerere ku Mau; kubwerera ku maziko a Paulo. Kubwerera kwa Yesu. Kubwerera ku mphamvu ya Mulungu. Kubwerera ku chiyambi. Pakhala pali tulukani wamkulu, ndipo pano tiri! Ine ndikukhulupirira kuti ife tiri okhoza kutenga dzikolo. Ine ndikukhulupirira kuti ife ndife okhoza kukhala Mkwatibwi kupenya mofanana, tonse kulankhula chinthu chofanana, popanda magawano pakati pathu, gawo lililonse kupereka kwa gawo lina zosowa zake, ndipo osagwedezekagwedezekanso ndi kutengeka ndi mphepo iriyonse ya chiphunzitso. Ine ndikukhulupirira kuti Mulungu anaika mu Mau Ake utumiki umene udzakhala pano pamene ife tidzafika kudziko... Ife titenga chimenecho, ndipo Mulungu, Mwiniyekha, akuziyambitsa izo ndi mau akulu a ulamuliro amene akugwedeza dziko.

Ine ndikufuna ndiwerenge ku Aefeso, chaputala 4. Taonani kuti Paulo anali atanena kale kuti watsala pang'ono kuchoka pa dziko. (2 Timoteo, chaputala 4:6-8) Iye anali ku ndende; iye amakonzekera kupita kumudzi. Koma Ambuye asanamutengere kumudzi, Mulungu anachita ndi Paulo, monga anachitira ndi Mose. Mose sanawatengere iwo uko ndi kukatenga dzikolo; iye anawauza iwo za dzikolo ndi kuwapatsa iwo Madera ena. Iwo analowa mu chipululu ndipo zaka 40 zitatha, iwo anabwereranso ndi kutenga dzikolo. Paulo anachitanso chimodzimodzi. Iye anaupatsa mpingo utumiki kuti apulumuke nawo, mpakana tidzafike kudzikolakwathu. Inde, nthawi ina Paulo anaika ma Bishopi, ma dikoni, ma edala ndi ena otero... (1 Timoteo, chaputala 3). Pokhala mu nthawi yomweyi pakati pa 64 A.D, Ndipo imfa yake (ena amati 66 A.D) Iye anamulembera Timoteo ndikumuuza choti achite mpingo utachoka kudzikolakwathu. (Kenanso, kumeneku ndi ku 1 Timoteo, chaputala 3 ndi Tito, chaputala 1) Iye anati, “Dzisankhireni inu (lozani) amuna ena kuti akhale ichi.” **Koma, tikafika ku utumiki uwu (Utumiki usanu) pamene tifika ku dzikolo, ndiye kusankha kwathu kwatha, chifukwa tiribe cholankhula pa zimenezo.** Paulo anati, “Ine ndinasankhidwa kukhala mtumwi kuchokera mu mimba ya amai anga.” Mukuona, iye anabadwa kukhala chimenecho. Inu mumabadwa kukhala chinachake. Kotero palibe masankho pa izo, kukuvoterani kapena kukuchotsani. Ndi Mulungu amene wakusonyani inu kuti muchite chinachake, ndipo zimenezo zimachikhazikitsa icho; ndipo zimangokupangani kukhala munthu woyenera pa ntchitoyo.

Kotero uku ku Aefeso, chaputala 4, ine ndikufuna kuyamba kuwerenga vesi 11. Paulo akuti, “*Pamene Khristu anakwera kumwamba Iye anapereka mphatso...*” Ine sindidutsa mu zonsezo chifukwa ife takhala tikudutsamo nthawi zambiri. Koma ine ndikufuna kutenga vesi 11 kumene akulankhula za utumiki umene Khristu akupereka. Akuti ku Aefeso 4:11 – “*Ndipo Iye anapatsa ena akhale atumwi; ndi ena, aneneri; ndi ena, alaliki; ndi ena, abusa ndi aphunzitsi;*” Tsopano awo ndi mautumiki otumikira asanu; ndipo mavesi oyambirira akuti, “Iye anapereka mphatso izi kwa amuna.” Kotero ku gawo lotsiriza la lofikitsa ku ungwiro, akazi akuchotsedwa mu gawo lolalikira. Tsopano inu musakhumudwe chifukwa ndi m'mene ziriri. Ndi gawo lotsiriza la izo, akazi mulibemo. Iye akuziika ku mautumiki asanu – atumwi, aneneri, alaliki, abusa, ndi aphunzitsi.

Ndiloreni nditenge vesi limene Iye anapereka mphatsozo kwa amuna. Vesi 8 – “Chifukwa chache anena, “*M'mene anakwera kumwamba anamanga ndende undende, naninkha zaufulu kwa amuna.*” “Amuna” pamene ndiye pamene pali chiyambi; sakuikamo akazi m'menemo mu chinthu ichi. Uwu ndi utumiki okhawa umene ine ndikuudziwa umene akazi sakuikidwamo. Chirichonse mwa mphatso zisanu ndi zinai-- uneneri, kumasulira, malirime, ndi zina zonse —iwo akhoza kuchita, monganso amuna. Chomwechonso, mphatso za mzimu ziri za onse amuna ndi akazi. Koma Iye akupatula chinachake (utumiki), chifukwa pali ntchito imene ikusowa kupanga lingaliro (utsogoleri) imene ikuyenera kukhala yoima; pamene ndi pamene mukhoza kudziwa, “Njirayo ndi iyi.” Ife tadutsa mu mibado kumene timanena: “Chabwino, zikanakhala njira iyi; zikanakhala njira iyo. Mlaliki uyu amazilalikira njira iyo ndipo ine ndimazikonda bwino; mlaliki uyo amazifotokoza njira iyo ndipo ine ndimazikonda bwino ndipo anali ndi lemba la ulaliki pa zimene amalankhula.” Chabwino, izo ndi zoono, koma kumapeto kwa m'bado, Iye akutibweretsera chimene Paulo ananena chidzakhala. Mukuona, ichi ndi chokhacho (ndipo sindingathe kuchifotokoza mokwanira), iyi ndi nthawi yokhayo imene ife tikufika pa malo amene ife sitingathe kugwedezekanso uku ndi uko, ife tonse tilankhula chinthu chofanana, ndikupenya mofanana, ndikumangirirana wina ndi mnzache. Nthawi yake ndi yomweyi – kuno ku mapeto. Kotero Iye anaika utumiki. Ife tikabwerera ku mudzi (apo chiri). Ife tikanatha kung'amba Aefeso, chaputala 4 ndi kuchotsa, ndi kuika mu matumba mwathu kudutsa mu mibado ya mipingo...., koma musamuononge. Mumutulutsenso mthumbamo tikafika ku dzikolakwathu; chifukwa ndi chimene Mulungu adzagwiritsa ntchito. Iye anagwiritsa ntchito Paulo, monga anagwiritsira ntchito Mose. Mose

sanawatengere iwo ku dzikolo, koma anawauza m'mene zidzakhali. Iye anamupatsa Kalebi phiri limenelo, ndipo Kalebi anati, "Mose anati ine ndikhoza kukhala nalo phiri limeneli." Iwo anazungulira mu chipululu kwa zaka makumi awiri, koma pamene anabwerera mau a Mose anali abwinobe. Kalebi akanakhala nalo phiri limenelo.

Mulungu anaika utumiki apa ndipo Iye anati, "Ichi ndi chimene ndidzagwiritse ntchito kufikitsa oyera mtima ku ungwiro." Ife tinazungulira mu chipululu ndipo tinalibe icho. Koma pamene ife tinafika ku ku dzikolakwathu, ndi ichi tsopano! Ndipo Iye akukwaniritsa maudindo mwa kudzoza amuna, kuwaika iwo m'menemo ndipo udindo uliwonse udzizindikiritsa okha. Koma taonani pamene tifika ku dziko lakwathu; Paulo anati, "Padzakhala mphatso zimene Iye adzapereka kwa amuna." Ndipo pamene izi zifika ndikuikidwa mu mpingo, ndiye imeneyo ndi nthawi ya kufika ku ungwiro (kapena ukulumsinkhu.) Izo sizimapita mu m'bado wina kuchokera kuno, chifukwa ife tafika ku uthunthu wa munthu Yesu Khristu, ife timafika ku chidzalo cha Khristu, ndipo ndi nthawi yokwatulidwa.

Tsopano ndiloreni ndiwerenge apa. Aefeso 4:11 – "*Ndipo Iye anapatsa ena akhale atumwi, ndi ena aneneri, ndi ena alaliki, ndi ena abusa, ndi ena aphunzitsi; vesi 12-* (Taonani) *ku ungwiro wa oyeramtima, ku ntchito ya utumiki, kumangirira thupi la Khristu: (Thupi liri mkati, lalowetsedwa, kubweretsedwa mkati ndi kuphunzitsidwa.)*

Vesi 13; (Tsopano taonani) "*Mpakana ife tonse...*" Taonani – aliyense amene ali mu thupilo amene maina awo analembedwa mu bukhu, Danieli anati, iwo adzapulumutsidwa. "*Mpakana tonse tikafike ku umodzi wa chikhulupiriro...*" Oh, mai, ine ndikuuzanu, Akuluakulu, ife tikudziwa kuti zimenezo sizinachitike, sichoncho? Koma akuti pamene utumiki uwu udzafika kuti izi ndi zimene zidzachitika. Inu mukafika ku dziko lakwanu, ichi ndi chimene chidzachitika. Inu mudzafika ku umodzi wa chikhulupiriro. Paulo analankhula ndi kunena, Ine ndikanakonda kwa Mulungu kuti nonse mulankhule chinthu chimodzi, kukhala ndi lingaliro limodzi, kukhala ndi chiweruzo chimodzi, ndi chikondi pa wina ndi mnzache." Koteri ife tafika ku dzikolakwathu. (Ife tidzatenga zimenezo ku Chivumbulutso 10:8 -11.) "*Mpakana tonse tifike ku umodzi wa chikhulupiriro, (taonani) ndi chidziwitso cha Mwana wa Mulungu, (tsopano taonani) ku ungwiro wa munthu...*"

Tsopano ameneyo ndiye Khristu, mpingo, ife timasandulika munthu wangwiro Khristu. Mwa kulankhula kwina, chimene Khristu anali mu ulemmerero- ndi chimene Mkwatibwi akuyenera kukhala. Ndipo, akuluakulu, ife tikhoza ngakhale kulora chikhulupiriro chathu kukula; chifukwa sitingathe kuzichita zimenezo mu njira chabe yawamba monga ife timachitira nthawi zonse, kumaponyerana (zibakera) wina ndi mnzache tikapeza mpata. Ine ndikukuuzani padzakhala alaliki amene aitanidwa. Taonani ichi apa, ife tikufika tsopano. Zonse izi ziri kumbuyo kwathu, ndipo sitingathe kubweretsa zolephera zathu mu chimenecho.

M'bale wathu wakhala apayu anali ndi maloto amene anali auzimu kwambiri. Iye analota kuti tonse tinali malo amodzi titavala zovala zoyera, ndiye zimaoneka ngati vinyo anali atakhetsedwera pa Malaya. Iye anangotenga dzanja lake, ndi kupukuta ndipo basi zinangogwa, ndipo zinangokhala zoyera mwangwiro. Ine ndikuuzani inu kuti padzakhala chinachake mu nthawi ino chimene chidzangogwa. Pamene uthenga uwu udzafika penipeni, zidzakhala monga mai wanga amakonda kupanga sopo. Iwo amaika red-devil Iye mu zimenezo. Pamene ife timagwira ntchito ku macheke (malo amene mitengo imadulidwa ndi kukonza matabwa) ife timatenga mikaka ya paini, (zinthu zayelo kapena zobiriwira mikaka zochokera ku mitengo ya paini) mu maovolosi athu. Sopo anali wolimba kwambiri ndipo amamata m'manja moti akanatha kuchotsa khungu ngati mutagwira izo. Sopo ameneyo amangoseka pine rosin. Sopo amangoseka zothimbirira zimene sopowathu lero sangachotse. Mai anali ndi poto wamkulu wakuda ndi kutenthetsa madzi. Iwo amatenga ndodo ndi kutakasa kwa maora awiri kapena imodzi, ndiye kenako amatenga chopukusira ndi

kumapukusa ndi manja awo. Iwo anali amphamvu. Akatsiriza ..., ataziviika pafupifupi kanai, zimayera.

Kotero ine ndikukuuzani inu kuti Mau a Mulungu akubwera. Ndipo akuti, “Kuti Iye adzatiyeretsa ife ndi kuchapa kwa madzi mwa Mau.” Iye anati sipadzakhalanso mawanga, kapena makwinya. Mau awa adzangowapangitsa iwo kugwa, sichoncho? Kotero ine ndiri pano kukuuzani, kuti ife tafika kudzikolakwathu. Ndipo penapake, ngati si usiku uno, ine sindikudziwa kuti zidzakhala liti, koma si kale kale, inu mukuyenera kukhala mu uzimu wanu, kulingalira kwanu, kuti tiri pamene Paulo analankhula. Ife tiri mu nthawi imene Mkwatibwi akubwera palimodzi. Ife tiri mu nthawi imene ife tikuzindikira kuti tiri amodzi, ndife gawo la wina ndi mzache. Inu mukangochotsa chala chaching’ono ichi ndikuchiika pansu, icho sichingachite chiri chonse, koma kuchiika mu thupi lanu chikhoza kuchita kanthu. **Kotero apa pali utumiki umene Paulo anaika ndipo anati, “Tsopano inu mudzafika ku dziko limeneli tsiku lina,” ndipo apo liri; ife tafika!**

Pakhala pali mau aulamuliro akulankhula kuchokera kumwamba kunena, “Pita katenge kabukhu kakang’ono tsopano.” Haleluya! Ife tikupita, ndipo lasamutsidwa mu dzanja la Khristu Mngelo Wamkulu, kupita ku dzanja la utumiki; koma sizinatero mpakana mau a ulamuliro atalankhula kuchokera kumwamba. Akulankhula kwa Yohane ndikumuuza iye, “Pita ukatenge kabukhu kakang’ono.” Pakuyenera kukhala kuitana mkatikati, chakuya chimayitanira chakuya. Davite nati, “Chakuya chimaitanira ku chakuya pa phokoso la madzi.” Mwa kulankhula kwina, pali chinachake chazimu kudutsa ku mbali yanu, kukusunthani ndi kukudziwitsani inu, kukuuzani kuti mufikire zambiri zoposa zomwe mwafikira, kuyang’ana mu mau ndi kutsegula maso anu a uzimu ndi kuyang’ana mozungulira ndi kuona ngati Mulungu akuchita chimene ananena adzachichita; kapena tikungosewera apa, ndi kungosewera chalitchi. Ine ndikukhulupirira kuti ndi nthawi imene ife tikuyenera kuwerenga kusonkhana kwathu kulikonse. Nthawi iriyonse pamene tikumana palimodzi, muziyese zopambana. Ndi nthawi yoyang’ana mozungulira ndikunena, “Ambuye, kodi mukuchita chimene izi zikulankhula, kapena takhala tikupusitsana tokha?” Takhala tikupusitsana tokha ngati sitingathe kutenga chikhulupiriro chimenecho ndi kuchikoka. Monga Yohane anati, “Khalani wolimbika kwambiri.” Ife tikuyenera kutenga dzikolo. Ndipo ine ndikukhulupirira ndi mtima wanga wonse kuti tsikulo ndi iri, nthawiyo ndi iyi imene Ambuye wabwera kutipatsa ife mphamvu yotenga dzikolo.

Iye anaika pamaso pathu utumiki umene udzatipangitsa ife mwa mtheradi kutenga dzikolo ndi chimene Mau anena kukhala chomwecho. Iwo analankhula za Paulo, “Iye ndi wofooka. Iye zolankhula zake ndi zosagwiramtima.” Uwu ndi umunthu, ndipo chinthu ichi ndi cha thupi. Koma abale ndi alongo, penapake ife tikuyenera kubweretsa Mulungu mu kachitidwe. Kodi Iye akuchita chinachake? Nanga ngati akutero, ndiye kakhaliidwe kakuyenera kukhala chimene Mulungu anaika, ndi amene Mulungu anamuika, ndi m’mene Mulungu anaziikira izo. Ife tiri pano kunena kuti “Ambuye, ife tiri pano kumva chimene inu mukuyenera kunena.”

Kotero mu masiku a zolemba za Paulo, iye analemba malangizo ena ofunika kwambiri ku mpingo. Iwo sanazitenge, koma iye analembera izo kwa ife. Mulungu amadziwa kuti tikubwereranso. Iye anatiuza ife m’mene kusandulika kudzakhaliire ndi zonse. Iye amadziwa kuti ife tikubwerera ku dziko. Ife apo tiri usiku uno. Ife tiri pano; ndipo mautumiki awa alipo pano, ndipo ali pakati pa Mkwatibwi. Pali utumiki uwu wa utumwi, pali utumiki uwu wa ubusa, ndipo pali utumiki uwu wa uphunzitsi umene umatenga Mau ndi kuphunzitsa. Pali atumwi, aneneri, alaliki, abusa ndi aphunzitsi. Mlaliki akhoza kulumpha ndikumenyetsa mapazi ake pamodzi ndi kukuwa kamodzi kapena kawiri, koma iye adzakhala ndi Mau. Iye sakhala chabe mtolo. Iye adzalumikizidwa. Iye adzalankhula zomwezo zomwe atumwi, abusa, ndi onse akulankhula. Iwo onse adzalankhula chimodzimodzi, vumbulutso lomwelo. (Iwo sadzatenga bukhu ndi kumango “werenga” zolembedwa), koma vumbulutso

lidzalembedwa mu mtima mwawo ndi mu lingaliro lawo. Iwo adzakhala ndi lingaliro la Khristu. Sipadzakhala kutaika mu chiphunzitso cha icho; chifukwa zikuyenera kuziona mofanana.

Iye akunena apa mu vesi 13 – *“Kufikira ife tonse tikafikira ku umodzi wa chikhulupiriro, ndi wa chizindikiritso cha Mwana wa Mulungu, kwa munthu wangwiro, ku muyeso wa msinkhu wa chidzalo cha Khristu:”* Ndipo inu simungapeze chopambana pamenepo. Kapu yadzaza. Inu ngati muonjeza kuika madzi pamene kapu yadzaza, zimangotaikira pa tebulo. Ndipo iye anati utumiki uwu ukukhala apa mu Mau, ndipo pamene mubwerera, ine ndidzakhala ndi utumiki kumeneko. Uli pompano. Amen. Anthu ali pompano. Yesu Khristu ali pompano, ndipo inu muli pompano. Pali kugogoda pang’ono pakhomo, **“Kodi mudzachita chiyani ndi Yesu uyu otchedwa Khristu?”** Iye amayenda pakati pathu. Iye watibweretsa ife ku dzikolakwathu, ndipo pali mau a ulamuliro amene akuti, *“Pita katenge ilo.”* Tiyeni titenge kukumana uku ngati nthawi ya mau a ulamuliro a Mulungu. Ine ndikukhulupirira kuti pafupifupi aliyense akumverera chinachake mu mtima mwake. Ambiri andiuzwa ine, *“Ine ndikukhulupirira kuti msonkhano uwu waikidwa ndi Mulungu. Ine ndikumverera ngati kuti Ambuye atilankhula ife.”* Kotero tiyeni tikhale ndi makutu athu auzimu otsegula.

Koma taonani, Iye anati *“Pamene mudzafika ku dzikolakwanu ndi kutenga utumiki uwu, inu mudzafika ku chidzalo cha munthu Khristu Yesu pansu pa utsogoleri wa utumiki usanu, monga m’mene Iye ananenera ku Bukhu la Aefeso. Pali amuna oyenera amene afika kutsogolo. Ngati inu mutawerenga, Yoshua anali munthu analozera njira yoolokera, ndipo anthu anatsatira. Koma panali akulu ankhondo pa pfuko lirilonse ndipo aliyense kugwira ntchito mu umodzi, ndipo iwo anatenga dzikolo.*

Tsopano ndi angati amene akuona – *“Kubwerera ku dzikolakwathu?”* Iye anati, *“Pamene mudzabwerera kwanu, ichi ndi chimene mudzakhala nacho. Ichi ndi chimene chikukuyembekezerani inu.”* Kodi mukudziwa chimene chiri? Ndi uchi. Umakoma ndithu; koma pali kuwawa mwa iwo pamene tiyamba kuzigwiritsa ntchito; chifukwa pali utumiki wa utumwi...Mukuona, iye anati zidzapita ku dziko lonse, kwa anthu onse, mafuko, ndi manenedwe, ndi mafumu (kapena maufumu.) Chabwino, tsopano Mulungu watsegula khomo ndipo pali kuthekera kotu mamirioni a wanthu ali ndi mwai kupeza uthengawu pa internet. Ma tepi akhala akupita kwa zaka makumi anai, ndipo zanenedwa palibe nthawi imene matepi awa sakuseweredwa pa dziko lapansi. Mulungu anati zidzakhala ku mafuko, anthu ndi manenedwe.

Tsopano ndiloreni nditenge ichi chonse. Taonani, ife tanafika ku kukulamsinkhu. Iye anati pamene inu mudzafikanso ku utumiki uwu inu mudzafika ku kukulamsinkhu, ndipo simungakulenso msinkhu kuposa pamenepo. Ndipo iye anati mu vesi 14 – *“Kuti tisakhalenso makanda, ogwedezekagwedezeka, natengekatengeka ndi mphepo ya chiphunzitso, ndi tsenga la anthu, ndi kuchenjerera kukatsata chinyengo cha kusocheretsa.”* Mau akuti, *“Inu simudzakhalanso ana ogwedezeka uku ndi uko ndi mphepo iriyonse ya chiphunzitso.”* Ngati wina aliyense ali ndi mantha akhoza kunyengedwa, zikutanthauza kuti sakudziwa chimene akuchita; chifukwa osankhidwa sadzanyengedwa. Mulungu adzakhala ndi china chake apa chimene sadzanyengedwa. Iwo adzadziwa kuti iwo akudziwa kuti alibwino, ndipo iwo adzadziwa kuti akudziwa chimene achikhulupirira chidzalumikizana ndi Mau kwathunthu...., ndipo akhoza kuona Mulungu kupanga Mau ake kukhala thupi pakati pawo. Paulo anati, *“Inu ndinu akalata olembedwa owerengedwa ndi anthu onse.*

Ine ndikukhulupirira ine ndikuona Mau kukhala thupi pamene ndiona inu; chifukwa inu mukukhulupirira Mau, inu mwadya Mau, ndipo mwasandulika Mau. Monga Yesu anali Mau osandulika thupi – Paulo anati, *‘Mau awa sanalembedwa mu magome a miyala, koma magome a minofu ya mitima.’* Inu ndi bukhu. Iye anati, *“Inu ndinu akalata olembedwa; inu ndinu kalata wanga. Inu ndinu umboni wanga. Inu ndi chimene ndabeleka.”* Mau asandulika

thupi; ndipo ndi inu, Mau a moyo a Mulungu, ndipo Mzimu umabwera ndi kufulumizitsa Mau ndi kuwapanga iwo kukhala amoyo monga m'mene anachitira ndi Yesu, pamene Mzimu unabwera pa Iye ndi Iye anati, "Lero lemba iri lakwaniritsidwa." Haleluya! Ndipo ndikukhulupirira ife tikhoza kunena, "Lero lemba iri lakwaniritsidwa." Pakhala pali mau a ulamuliro akulankhula, "Pita, tenga bukhu mu dzanja la Khristu." Choyamba mukuyenera kudziwa kuti Khristu ali pompano.

Panali m'bale wokondeka mu dziko, ndipo Mulungu anamutenga iye chaka chatha. Dzina lake ndi Raymond Jackson, ndipo uthenga wache unali, mwa zina, kumulora Mkwatibwi wa Amitundu kudziwa kumene Abale, (amene ndi Ayuda) ali mu dongosolo la Mulungu mu nthawi yotsiriza. Iye tikudziwa bwino lomwe pamene Israeli ali mu dongosolo la Mulungu, chifukwa cha gawo la uthenga wa M'bale Jackson umene anabweretsa kwa ife. Mulungu ndi wachisomo chopambana, Iye anatumiza munthu kudzamuonetsera Mkwatibwi kwa Abale. Mulungu anamutenga M'bale Jackson pa dziko chaka chatha, ndipo ife tinali ndi chisoni. Iye anagwira ntchito yake ndipo anaigwira bwino. Pamene mbiri ya mpingo idzakhala ikulembedwa, ndi zimene Mulungu wachita, inu mudzapeza dzina la M'bale Jackson pamwamba penipeni, ndi mau oti "Munthu uyu anagwira ntchito, ndipo inali ntchito yapamwamba." Tsopano Mkwatibwi wadziwitsidwa kwa Abale, ndi kuuzidwa za mu nthawi yotsiriza.

Mulungu atatha kugwiritsa ntchito M'bale Branham kudziwitsa Mkwatibwi kwa Khristu..., ndipo Khristu akuti, "Ine ndiri nawo Abale; Ine ndikufuna ndikuuze za Abale amenewo. Ine ndikufuna iwe kuti udziwe za Abale anga." Monga Yosefe, mosakaikitsa anamuza Mkwatibwi wake wa Amitundu za abale; koteronso Mulungu anamulora Mkwatibwi kudziwa abale ake. Anthu awa abwino a Mulungu, Ayuda, adzatenganso uthenga pamene Mulungu adzatumiza aneneri awiri kunenera ndi kutulutsa 144,000 ndi uthenga. Ngati inu mutati mulandire pepala lotchedwa Contender ndi kutenga matepi a M'bale Jackson, inu mudzamva munthu akulankhula za Israeli. Inu mudzamva munthu akulankhula za "Uthenga Wosatha ndi Ayuda 144, 000 amene akuyenera kulalikira izo." Inu mudzamva munthu amene akulankhula za, "M'bado wa kukonzanso." Inu mudzamva za munthu amene akulankhula za "Mkazi Wodabwitsa – Chivumbulutso chaputala 12." Inu mudzamva munthu akulankhula za "Masabata makumi asanu ndi awiri a Danieli," m'mene kachisi amangidwire, ndi zimene zidzachitike ku Israeli, ndipo mudzamva munthu amene akutiuzza ife m'mene adzatengera phazi lililonse la dzikolo. Inu mudzamva munthu akutiuzza ife kuti Mulungu posachedwapa amupatsa Israeli chigonjetso chopambana, ndipo iwo adzagonjetsa chipembedzo cha chisilamu. Ngakhalenso Saudi Arabia amene ndi ana a Abraham mwa mkazi wake wachiwiri adzabwerera ndi kubweretsa siliva ndi golide ndi kumanganso kachisi yemweyo, chifukwa iwo ndi ana a Abrahamu mwa mkazi winayu. M'bale Jackson anazipanga izi kudziwika kwa Mkwatibwi, Abale (Israeli.)

Kuno ku United States of America ndi kumene angelo asanu ndi awiri anatsika, kumene Mulungu anatumiza mneneri ndi uthenga wa kwa Amitundu, ndipo tsopano ife tichita chiyani? **M'bale Branham iye wapita, iye sabweranso. M'bale Jackson wapita, ndipo iye M'bale Jackson anazisiya izo kuti chisindikizo chachisanu ndi chiwiri sichinamasulidwe. Iye anazisiya kuti Mngelo Wamkulu wa ku Chivumbulutso chaputala 10 sanapfuule, ndipo mabingu asanu ndi awiri sanaombe. Iye anazisiya mu njira imeneyo.** Mulungu anadzala chimenecho pamenepo; ndi molondola monga m'mene Mulungu anazisiyira. Ine ndikukweza dzanja langa kwa Wamphamvuzonse ndi kunena, "Ndikuyamikira njira zanu, Oh Mulungu; chifukwa njira zanu ndi zovuta kuzimvetisa. Ndi zodabwitsa, ndi zapamwamba; zodabwitsa kuzilankhula." Koma apo ife tiri. Ziri zowala ngati khristalo kwa ife. Iye tsopano tikuwadziwa abale; ife tikudziwa malo athu, ndipo timawakonda Abale athu. Inu simungalankhule choipa chokhudza Israeli ndi kumusangalatsa Mulungu. Mulungu anatumiza munthu (Raymond Jackson), ndipo iye

anafikira ndi kutionetsera Israeli m'mene iye akulumikizirana mu banja la Mulungu. Iwo ali ndi malo awo. M'bale Branham choyamba anationetsera ife kuti Ayuda anali abale athu pamene chisindikizo chachisanu chinatsegulidwa, koma apo pakubwera Mulungu akudzutsa M'bale Jackson kuti atiuze ife tonse za iwo, komanso anafotokoza bwinobwino (kuziwonetsera m'malemba) zambiri za ziphunzitsa za M'bale William Branham.

Taonani tsopano Mau akunena ku Aefeso, chaputala 4:14, "Ife sitikugwedezeka gwedezekanso uku ndi uko ndi kutengeka ndi mphepo iriyonse ya chipembedzo;" ife sitinganyegedwe. Taonani vesi 15..., (izi ndi zimene alaliki ambiri adzachita, chifukwa sadzasowanso kuchita mosiyanasiyana.) Lorani zimenezo zilowerere pang'ono. Izi ndi zimene alaliki adzachita, chifukwa iwo sadzasowanso kuchita mosiyanasiyana. Ife sitikuyenera kumenya anthu pa mutu. Ife sitikuyenera kukutembenezani dzanja lanu ndi zina monga choncho. Ife sitikuyenera kutsina makutu anu ndi kukoka mphuno zanu. Ichi ndi chimene alaliki akuchita, chifukwa iwo sakusowa kuchita mosiyana. Vesi 15 – ***"Koma kulankhula zoonu mu chikondi..."*** Inu simudzasowanso kulankhula mosiyana, chifukwa thupilo lasonkhanitsidwa mozungulira inu. Inu mumawakonda iwo; inu ndinu gawo la inu. Ndi cholinga chanu kuti iwo akhale ndi chapamwamba, ndipo chifukwa chakuti inu mukufuna iwo akhale ndi chopambana, inu mumawapatsa iwo zabwino zanu. Ine sindikudziwa m'mene aliyense aliri bwino mwa kuzindikira mitima, koma ine ndabwera ndikukupatsani chopambana changa. Ine ndabwera kudzazikhuthula ndekha.

Pamene ine ndinali ku Afrika ine sindinasungapo iriyonse ya mphamvu zanga. Ine ndinapereka zonse pa cholinga. Pamene ndinali mu ndege panalibe chimene chinatsala. Koma panali miyoyo yochepa imene inanena, "Mungabwere ndikudzatithandiza?" Ine ndinakhuthula zonse. Ine sindinasiye chirichonse. Ndipo ndi chimene ndikuchita usiku uno ndi chimene ndinachita usiku watha. Ine sindikusunga chirichonse. Ine ndikuzikhuthula ndekha kwa inu. Ndi kunena, "Tisalore mwai uwu utiphonye." Ife sitingazibweze ndi kumanena kuti zidzakhala tsiku lina. Ife talankhula zimenezo kwa nthawi yaitali, koma tsopano Iye watibweretsa ife ku dzikolo.

Tsopano taonani chimene utumiki udzachita. Vesi 15 – ***"Koma ndi kuchita zoonu mwa chikondi tikakule m'zinthu zonse, kufikira Iye (Yesu) amene ali mutu ndiye Khristu; Vesi 16 – Kuchokera kwa Iye thupi lonse, lokowanidwa ndi lolumikizidwa pamodzi, pothandizanapo mfuno yonse..."*** Ine ndimazikonda izo. Ife timapatsana mphamvu wina ndi nzache. Ine ndinapita ku malo kukalalikira kumene iwe sungatenge mphamvu, koma pamene ine ndiona kumwetulira pang'ono, ndikumamva Amen pang'ono, zimangozipanga izo kukhala bwino. Zimakhala ngati kuti mukumenyana ndi kumenyana ndi mphepo. Pali gulu lokhala ngati siponji limene limayamwa, chifukwa chirichonse chimene chinali chitathiridwa mu siponji sichinali chabwino kuti chilowe. Ndicho chifukwa chake ife tikubwereranso ku chiyeero cha Mau, ndi chiyeero cha alaliki ena amene ali olorera kupereka zonse. Inu musasiye chirichonse. Paulo anati, "Inu ndinu ulemmerero wanga." Pamene ndichoka pano ndikupita ku chipinda changa sinditsala ndi chirichonse mwa ine; ndikhala nditakhuthula zonse, kutulutsa zonse, ndipo mokondwa ine ndichita izo. Mokondwa ine ndipereka, kupereka kuchotsa, kuti uthenga upite patsogolo pang'ono. Ine ndikukhulupirira usiku uno kuti ife timva mau a ulamuliro a Wamphamvuzonse. Mukuona, pali kumverera kumene kumabwera mkati mwanu. Inu mumamva atate akuti, "Pita katenge kabukhu kakang'ono." Ndipo inu mumayenda kupita kwa Mngelo Wamphamvuzonse ndi kunena, "Ndipatseni kabukhu kakang'ono." Ndi mau aulamuliro kukuuzani inu kuchita chimenecho. Zikuyenera kukhala mu Mzimu. Si chinthu cha thupi. Inu mudzadziwa, "Hey, ichi ndi cheni cheni."

Kupitiriza ndi vesi 16 – ***"...monga mwa kuchititsa kwa chiwalo chonse pa muyeso wache, lichita makulidwe a thupi, kufikira chimango chache mwa chikondi."*** Zimafika pa malo pamene zimayamba kumangirirana wina ndi nzache. Abale ndi alongo, ndi ntchito yanu kuyamba kumangirira abale ndi alongo ena mu thupi. Inu mukuyenera kumangirira.

Sikungoti, timayembekezera mlaliki kubwera ndi kudzatipanga ife ndikutigwedeza ndi kutidzutsa, zimenezo ndi zabwino. Ine ndiri okondwa kuulora Mzimu Woyera kundigwiritsa ntchito..., koma penapake mukuyenera kumangirirana wina ndi mnzache. Ife tikuyenera kubwezana wina ndi mnzache chifukwa tiri amodzi. Thupi limadzimangirira lokha mu chikondi, ndipo membala aliyense amatengapo mbali. Ife ndife amodzi. Ife taoloka Yordano kupita ku dziko labwino la Kenani, ndipo izi ziri ngati kumwamba kwa ine. Amen. “Ndi ena kudutsa mu madzi, ena kudutsa mu moto, koma onse kudutsa mu mwazi.” Iye watonkhanitsa tsopano. Iye watibweretsa kumudzi, ndipo dzikolakwathu ndi Mau. Paulo analankhula izi, **“Inu mwafika ku Yerusalemu wamwambamwamba. Inu mwafika ku makamu osawerengeka a angelo. Inu mwafika ku mizimu ya amuna olungama yopangidwa mwangwiro. Inu mwafika kwa Yesu, nkhalapakati wa pangano labwino.”**

Inu mwafika ku mizimu ya anthu olungama yopangidwa mwangwiro – chotchinga, khoma limenelo likucheperachepera pakati pa amoyo ndi akufa. Mulungu anamugwiritsa ntchito Mneneri William Branham kupitako. Iye anati, “Ine ndinayang’ana pa bedi ndipo apo panali thupi langa. Zimaoneka ngati kuti ndinali pafupifupi mapazi khumi ndi asanu kudza atatu, ndipo apo ndinali ndi onse oyeramtima amene anapita kale.” Iye anati, “Si mtunda koma ndi deralina.” Paulo anati, “Mwafika ku makamu osawerengeka a angelo.” Ndipo Mau akuti mu malo ena, “Angelo a Ambuye amawazungulira iwo amene awopa Mulungu.” Ngati titati talora chikhulupiriro chathu chikhale pa mapako a mphungu, tikhoza kukhala pa mapiko a chikhulupiriro ndi kufunsa zinthu izi zimene Mulungu wapereka. Ndi angati amene akukhulupirira kuti tafika ku dziko lakwathu? Paulo asanachoke, iye analemba m’mene kwenikweni zidzakhali. Siungakhale utumiki wina. Inu munali nawo mautumiki anu ena... Koma tsopano, Iye akufikitsa ku ungwiro Mkwatibwi ndi utumiki usanu. Utumiki wina uliwonse ukhoza kukhala wa iwo amene sali gawo la Mkwatibwi. Ine ndikumverera ngati angelo a Ambuye ali pompano usiku uno.....ndipo ndi nthawi yathu kusiya kusautsika; koterotiyeni tidye ndi kukhuta kuchokera ku gome la Mulungu usiku uno. Mulungu akudalitseni ndilo pemphero langa. Amen

## MAU A ULAMULIRO

March 19, 2006  
Glen Fork, West Virginia (USA)

Tiyeni titsegule ku Mau a Mulungu ku chaputala cha khumi cha Bukhu la Chivumbulutso.

Tisanawerenge ine ndikufuna ndifotokoze maloto amene ndinali nawo masabata ochepa apitawo; ine ndimalalikira zina pa za mibado ya mpingo ndi kumabweretsa mfundo zina za mu mbiri. Koma usiku wina nditangotha kulalikira mauthenga angapo, ine ndinali ndi maloto kuti ndinali mu chinachake ngati nyumba ya kuwala, ndipo anthu osiyanasiyana anali kubwera ku nyumba ya kuwala imeneyi ndipo iwo amabwera chifukwa kuwalako kunali kumeneko, koma kunalibenso kuwala ngati kumeneko. Pamene ine ndinali kupita, ine ndimalingalira ndekha, “Iyi ikhala nthawi yanga yotsiriza kubwera kuno.” Mu maloto, anthu amabwera ku chinthu chimene chinaliko, osati chimene chiri, mukuona. Ndi zabwino kudziwa zinthu izo zimene Mulungu wachita, koma Iye ndi **Mulungu wa lero**, ndipo ali okhoza kuchita moposa ndi mochuluka pamwamba pa chirichonse chimene ife tingafunse kapena kulingalira. Ife tikungoyamika Mulungu kuti akusuntha mu njira yapadera.

Koma mu maloto awa; ine ndinati, “Ine sindibweranso kuno.” Kotero ine sindidzatenganso mauthenga ochuluka ndikupita mwakuya mu mbiri ya zinthu zokhudza mibado ya mpingo. Komai ine ndidzati, “Ife tadutsa mu mibado ya mpingo isanu ndi iwiri ndipo iyo yatha, iyo ndi mbiri ndipo ndiri okondwa kuti ife tikuzidziwa izo.” Koma kukutengani ndikukusungani nthawi yayitali kukuphunzitsani maphunziro okhudza mbiri, ndikumakuonetsera kuti wam’thenga anali ndani ndi kuti mngelo anali ndani zinthu zina zotere, ine ndikukhulupirira kuti Ambuye akuti, “Usapitenso kumeneko.” Gawo limenelo latsirizidwa, gawo limenelo latha, ndipo gawo limenelo latheka; ife tikupita ku zinthu zazikulu. Komanso, ine ndikufuna kufotokoza maloto ena. Pamene ine ndimakonza Bukhu Lomasuliriridwa la Chivumbulutso; ine ndimawerenga chaputala cha khumi, ndipo ine ndinali ndi maloto: Mu maloto amenewa ine ndimadutsa malo omwetera udzu ndipo kunali udzu wobiriwira pozungulira, ndipo panali katerera kakang’ono koyenda munsewu ngati wagoni. Panali nyumba ya pa munda ndipo pamene ndinayandikira iyo, nyumbayo imaoneka ngati panalibe munthu amene amakhalamo. Ine ndinalingalira kwa ine ndekha, “Ine ndiyenda moyandikira nyumba imeneyi yakaleyi...,” ndipo pamene ndinatero, mwadzidzidzi chitseko chinatseguka ndipo panatuluka munthu. Ine ndinawona anali ndi china chake mu dzanja lake ndipo ndinayang’ana, ndipo ndinaona kuti inali nyanga ya ng’ombe, monga wapolisi amachitira kapena winawake amene akulengeza kwa anthu. Iye anatuluka kufika kumapeto kwa khonde ndipo anayika kukamwa kwake, ndikuyang’ana molunjika kwa ine; iye analankhula mokweza, “**KUMBUKIRA MAPAZI.**” Kenako iye anatsitsa nyangayo pansu kuchotsa kukamwa kwake ndikuigwira chambali, ndiye analowanso nyumba ndi kutseka chitseko. Kenako ine ndinadzuka.

Ine ndinayamba kudabwa nazo, ndipo zimaoneka ngati zikubwera kwa ine, chaputala cha khumi cha Bukhu la Chivumbulutso. “Kumbukira mapazi.” Mu chaputala cha khumi ichi cha Chivumbulutso, mapazi ndi ofunika kwambiri. Iye akuika phazi Lake la kumanja pa nyanja, ndipo phazi Lake lakumanzere pantunda.

Tsopano zakhazikitsidwa momveka bwino mu Mau a Mulungu kuti Nyanja ikutanthauza “khamu la anthu,” chimene chikuimirira kubwera kwake kumayambiriro mu mibado ya pentekosite kwa anthu a kum’awa. Koma phazi la kumanzere likutanthauza “malo achipululu ochepa anthu,” chimene chikuimirira kubwera kwake kuno ku United States. (Ku Ulaya ndi madera ena, USA amadziwika ngati “pfuko la kuchipululu” kalekale.) Mu 1963, Khristu anabwera pa dziko lapansi ndi kudzakwaniritsa “**phazi lina pantunda**” potumiza angelo asanu ndi awiri, ndipo Zisindikizo zinauluridwa. Izi zadziwika kwa ife mwa

kuphunzitsa kwa M'bale William Branham m'mene iye amabweretsa vumbulutso iri la United States 'kukhala Chirombo Mwanawankhosa chimene chikutuluka pansa pa dziko'- "limenelo ndi gawo la dziko."

**Kumbukira mapazi** – Tsopano kuyambira nthawi imene iye anaika phazi Lake lamanja pa nyanja ndi phazi Lake lamanzere pa mtunda, padutsa pafupifupi zaka zikwi ziwiri, ndipo kudutsa mu nthawi imeneyo, mibado ya mpingo yatha ndi kutsirizika. Iyo ikuyamba ndi kutsirizika mu nyengo ya nthawi imeneyi. Iye tikupeza kuti mapazi ndi ofunika kwambiri, ndipo ngati ife tiphonya mfundo imeneyi, ife tiphonya chinthu icho cha Chivumbulutso, chaputala cha khumi, ndipo ndi nthawi yochiona icho. **Ndi pafupifupi nyengo ya zaka zikwi ziwiri pakati pa phazi limodzi pa nyanja ndi phazi lina pa mtunda.** Ndipo pamene Mngelo Wamkulu akutsika, Iye ali ndi bukhu lotsegula. Ndichidzalo cha Khristu. Iye akutibweretsa ife chidzalo cha Iyemwini.

Bukhu iri laling'ono linali lotseguka ku mpingo woyamba ndipo kabukhu kakang'ono ndi Mau a Mulungu. Paulo anati, "Inu ndinu akalata wolembedwa owerengedwa ndi anthu onse." Mau a Mulungu amatiphunzitsa kuti lemba limapha, koma Mzimu upereka moyo. Paulo anati, Mulungu watipanga ife atumiki wokhoza a ku Chipangano Chatsopano (chimene chinali chisanalembedwe mu nthawi imeneyo) osati a lemba la Mau koma a Mzimu." **Kotero lemba linasandulika mtengo wa Chidziwitso cha Mau,** koma Mzimu wa moyo wa Mau amenewo ulipo kwa ife lero – "umenewo ndi Mtengo wa Moyo."

Tsopano pamene tikuwerenga ichi, ine ndikufuna inu muone chinachake apa. Ine ndiyamba ndi kuwerenga vesi loyamba, koma lingaliro langa lenireni likhala pakati pa mavesi 8 ndi 11. Pamene tikuwerenga apa, ife tibwerezanso zina zomwe tadutsamo usiku uja, kungokumbutsa malingaliro anu. (Chivumbulutso 10:1) Akuti, "*Ndipo ndinaona mngelo wina wolimba alikutsika Kumwamba, wobvala mtambo: zikutanthauza kuti zikutengera vumbulutso kumuona Iye. Iye waphimbika (kapena wabvala) mtambo...*" *ndi utawaleza pa mutu pake,* (Mngelo wa Pangano) *ndipo nkhope yake ngati dzuwa, ndi mapazi ake ngati mizati yamoto:* (taonani: "mapazi ngati mizati yamoto" zikuonetsera kupezeka kwake pa dziko) zimenezo zikutizindikiritsa kuti ndi Ambuye Yesu Khristu mu maonekedwe a mngelo, ndipo pamene Iye abwera mu maonekedwe a mngelo, inu simungamuone ndi maso anu athupi. Ngati Mngelo zikutanthauza kuti, Iye akubwera mu maonekedwe a mngelo (kubwera kwa uzimu), ndipo Iye akubweretsa Mau a Uzimu kwa anthu.

Tsopano taonani vesi 2; akuti, *Ndipo anali nako m'dzanja lake kabukhu kofunyulula: ndipo anaponda nalo phazi Lake lamanja panyanja, ndi lamanzerelo pa nyanja....*, tsopano izi zinali mu 96 A.D, pamene Yohane amaona izi pa chisumbu chotchchedwa Patmo, ndipo iye anali pomwepo kuona izi zikuchitika. Tsopano Mngelo Wamkulu anali nako m'dzanja Lake kabukhu kakang'ono, kotsegula – Iye anabwera ku mpingo woyamba mu mphamvu ya Mpulumutsi woukitsidwa. Iye anabwera ku mpingo woyamba mu ulemmerero wake onse ndipo odwala onse amachiritsidwa, akufa amadzuka ndipo zodabwitsa zamphamvu zinachitika.

Ndiye taonani apa pamene tikuwerenga pamunsi pake; vesi 3 – *Napfuula ndi mau akulu, monga ngati mkango ubangula; ndipo pamene anapfuula mabingu asanu ndi awiri analankhula mau awo.* Tsopano ku chaputala choyamba cha Bukhu la Chivumbulutso kuyambira vesi 4; ife tikupeza kuti Mizimu isanu ndi iwiri ya Mulungu ikulankhulidwa koyamba mu Chipangano Chatsopano. Izi zikuchitika mu 96 A.D, mu tsiku la Yohane. Inde, ndi pamene angelo asanu ndi awiri (Mizimu isanu ndi iwiri) inalankhula mau awo ndipo Yohane anamva zimene iwo analankhula. **Tsopano ife tikumva kulankhula kwa mau amenewa monga zaululidwira mu tsiku lathu, ndipo ife timalandira ubwino wa izo. Ife tikumvetsa uthenga womwe analankhula.**

Tsopano vesi 4 akuti, *Ndipo pamene adalankhula mabingu asanu ndi awiri, ndinati ndilembe:* tsopano taonani, apa pali mau a ulamuliro pamene Mulungu akulankhula ndi Yohane mu 96 A.D, ndipo akumuza iye kuti asindikize zimene wazimva. Mau a ulamuliro

amene akulankhula ndi Yohane ndimau a Mzimu wamuyaya pamene akulankhula kupyolera mwa mamuna Khristu Yesu, amene akukhalabe pamwando wa Atate wachifumu. Kotero Mulungu Wamphamvu akulankhula ndi ulamuliro, mau olamula ndi kumuuza Yohane kusindikiza chimene mabingu alankhula.

Tsopano taonani pamene tikuziwerenga apa, vesi 4, *Ndipo pamene adalankhula mabingu asanu ndi awiri, ndinati ndilembe; ndipo ndinamva mau ochokera kumwamba nanena, Sindikiza nacho chizindikiro zimene adalankhula mabingu asanu ndi awiri ndipo usazilembe.*” Ine ndikufuna inu muone, mu 96 A.D. Mulungu anati, Sindikiza nacho chizindikiro. Mabingu atangotha kulankhula mau awo, Iye anati, “Sindikiza nacho chizindikiro zimene mabingu alankhula.” Zinali zoti zisindikizidwe mpakana mu nthawi ya kumapeto, ndipo Mulungu kenako akanadzatzsegula ndikuzipanga izo kudziwika kwa anthu a mu nthawi yotsiriza, chifukwa Iye akanakhala weniweni kwa anthu a munthawi yotsiriza, monga m’mene Iye anali mu mpingo woyamba.

Taonani tsopano, kudutsa mu mibado ya mpingo bukhu linali losindikizidwa, koma mibado ya mpingo isanayambe, kunali bukhu lotseguka; Khristu (Mau odzozedwa) anali wotseguka kwa anthu mu mpingo woyamba. Mu 96 A.D, Yohane analemba kuti iwo anali atagwa kale ku chikondi chawo choyamba. Iye anati, “Iwe wagwa.” Chivumbulutso, chaputala chachiwiri, pamene amalemba m’busa wa mpingo kumeneko, mngelo wa mpingo wa ku Efeso; Iye anati, “Iwe wagwa.” Kotero mpingo unali utagwa ndipo anataya chiyambi, iwo anataya moto, iwo anataya changu, iwo anataya Mzimu uja okhulupirira kuti zonse ndi zotheka kwa iwo amene akhulupirira. Iwo anataya chikhulupiriro chimene chiri chikuti zonse ndi zotheka kwa iwo amene akhulupirira. Iwo anataya kutumidwa kwawo, chiritsani odwala, dzutsani akufa, tulutsani ziwanda, kwaulele mulandira kwaulele mupereke. Mphamvu ya Mulungu inali mu mpingo mpakana Petro amatha kuyenda mu msewu ndipo iwo amaika odwala mu msewu, ndipo chinthunzi thunzi chake kuwakhudza iwo kunali ngati kukhudzana ndipo iwo amaonetsera chikhulupiriro chawo ndipo odwala amachira. Haleluya! Petro anadzutsa akufa, Paulo anadzutsa akufa, ndipo mpingo unali Mau. Paulo analemba, “Inu ndinu akalata anga wolembedwa owerengedwa ndi anthu onse.” Iye anati Mau awa sanalembedwe ndi inki, koma mu mitima yanu – kutanthauza kuti sizogwirika, Mau wowerengeka, koma ndi anthu eni kukhala Mau. Ndi Khristu kukhala mwa dziko, yemweyo dzulo, lero ndi kunthawi zosatha. Anali Yesu Khristu weniweni pakati pa anthu.

Mpingo woyamba unakhala pafupifupi zaka makumi anai wopanda Chipangano Chatsopano cholembedwa mu Baibulo chogwirika, chokhacho chimene anali nacho chinali Chipangano Chakale. Kenako mu 37 A.D., bukhu ka Mateyu linalembedwa, ndi chimene Paulo analemba (makalata ake) ku mpingo anachuluka iye atachoka pa dziko. Iwo amayenera kuchita mwa kutsogozedwa ndi Mzimu Woyera pa nthawiyo, monga Khristu analiri mu mpingo kutsogolera mpingo mkatikati. **Kotero tikhoza kunena kuti bukhu linatsegulidwa. Limayenera kutsegulidwa..., lisanatsekedwe ndi kusindikizidwa. Palibe chimene chinali chosadziwika, panalibe chobisika, panalibe chosindikizidwa; zinali kuti zonse ndi zotheka kwa iwo amene akhulupirira ndipo zinali zopezeka kwa iwo..., mpakana mpingo unagwa ndipo Khristu amayenera kuchoka mu njira imeneyo. Kenako ife tikuona Iye ngati Wamsembe Wamkulu kudutsa mu mibado isanu ndi iwiri ya mpingo. Izi zikutchulidwa ngati bukhu losindikizidwa.**

Ife tikuona ku Chivumbulutso, chaputala choyamba; kuti Iye wavala chovala chofika ku mapazi ake ndi lamba wa golide m’chiuno mwache; chimene chikutionetsera ife kuti Iye wavala chovala ngati Wamsembe Wamkulu. Taonani kuti ntchito ya Wamsembe Wamkulu inali yopereka mapemphero chifukwa cha zolakwa za anthu, ndipo anthu anali mu kulakwa. Tirigu ndi nansongole zinayamba kukulira limodzi, ndipo moyo wa Mau, Khristu unasindikizidwira kunja, sunali wopezeka mu maonekedwe amenewo mpakana nthawi yakumapeto; ngakhale kuti panali nthawi kudutsa mu mibado ya mpingo pamene Mulungu

amayenda pakati pawo. Komabe yambiri ya mipingo yathu inayamba kukhulupirira mu utatu ndipo amabatizidwa mu dzina la Atate , Mwana, ndi Mzimu Woyera (kungogwiritsa ntchito maudindo, ndipo osatchula dzinalo) ndipo Ambuye adalitse mitima yanu oyeramtima inu, ife tikakafika kumeneko tikaonana nawo, iwo amene maina awo ali mu bukhu la moyo. Koma mu tsiku lotsiriza, ife tikuyenera kupita ku chiyambi kumene bukhu linali lotsegulidwa, ndipo tikufika ku Mtengo wa Moyo umene unatengedwa ndi kupita ku paradaizo wa Mulungu ndi kubisidwa kwa ife. Izi ndizo tanthauzo la zisindikizo zisanu ndi ziwiri.

Tsopano kufika ku mfundo ndi kukhazikitsa funso kamodzi ndi kunthawi zonse lokhudza mabingu, kodi iwo awomba? Inde, iwo anaomba ndipo anasindikizidwa mu 96A.D. Tsopano tiyeni tiwerenge zimenezo kuti tikhale okhazikika, chifukwa sitikufuna kumangobwereza bwereza; pamene **uthenga** uwu ukuzipanga izo kukhala zosafunika kutero. Vesi 4 kachiwirinso, “*Ndipo pamene adalankhula mabingu asanu ndi awiri, ndinati ndilembe; ndipo ndinamva mau ochokera kumwamba nanena, Sindikiza nacho chizindikiro zimene adalankhula mabingu asanu ndi awiri ndipo usazilembe.*” Kotero pamene tikuona, **zakhazikika tsopano**. Bukhu linasindikizidwa ndi zisindikizo zisanu ndi ziwiri ndipo chinthu chokhacho zisindikizo zinanena mu Bukhu la Chivumbulutso chinali; “kavalu woyera,” chisindikizo choyamba, chisindikizo chachiwiri, “kavalu wofiira,” chachitatu chinali “kavalu wakuda,” chisindikizo chachinai, “kavalu wotumbuluka,” ndi kumapita m’munsi mu mzere...., ndi zomwezo zimene ife timazidziwa. Inali nthawi imene inasindikizidwa, kuyembekezera kufikira Khristu anali atatsiriza kupereka msembe ya oyeramtima. Tsopano zaka zikwi ziwiri zitatha, Iye akubweranso mu Mzimu kutikonzekezetsa ife kubwera kwake kwachiwiri mu thupi. Tsopano Iye alankhulanso ku Chivumbulutso chaputala 10:8 ndi mau omwewo a ulamuliro amene analankhula kwa Yohane pa vesi 4 ndikuti, “Sindikiza bukhu,” ndiye kenako mu vesi 7 akumuuzza iye nthawi imene adzamasula chisindikizo – “**Koma m’masiku a mngelo wachisanu ndi chiwiri.**” Inde, Iye akuyamba ntchito iyi potumiza m’neneri wamthenga ku m’bado uwu ndipo iye analalikira zisindikizo zisanu ndi ziwiri, ndipo kenanso ife tikumva mabingu akuomba. Mabingu sichina chirichonse koma “mau” a angelo asanu ndi awiri amene anali pomwepo ku Chivumbulutso, chaputala choyamba (kumene amatchedwa mizimu isanu ndi iwiri).

Kotero kuti tsopano kuti zonse izo zaululidwa; ife tikuona kuti zisindikizo zachotsedwa pa bukhu, ndipo bukhu ndi la Uzimu, ndi Khristu, Mau; chifukwa mngelo wauzimu anabwera, ndipo Iye sikuti akubweretsa bukhu lenireni. Bukhu lenireni sirinabwere; zinali mu Mzimu; moyo wa Khristu, Mtengo wa Moyo. Bukhu iri lenireni apa – Baibulo, ndi Mau a Chidziwitso; lasandulika Mtengo wa Chidziwitso ndipo seminare ina iriyonse ikugwiritsa ntchito kubweretsapo mzeru zawo ndi zina zotero. Koma Khristu tsopano wabwera ku dziko kudzakhala weniweni kwa anthu ndi Mau Olankhulidwa, amene ndi mbewu ya pachiyambi. Bukhu limenelo, moyo wa Khristu ndi wotseguka ndipo tsopano ife tikhoza kukhulupirira kuti zinthu zonse ndi zotheka.

Vesi 5 ndi 6 akuti, “*Ndipo mngelo amene ndinamuona alikuimirira pa Nyanja ndi pa mtunda, anakweza dzanja Lache lamanja kuloza kumwamba, nalumbira kutchula Iye amene ali ndi moyo ku nthawi za nthawi, amene analenga m’mwamba ndi zinthu ziri momwemo, ndi dziko lapansi ndi zinthu ziri momwemo, ndi dziko lapansi ndi zinthu ziri momwemo, ndi Nyanja ndi zinthu ziri momwemo kuti sipadzakhalanso nthawi...*”

Tsopano, pofuna kumvetsa vesi lachisanu ndi chimodzi, apa pali kiyi wofunika kwambiri. Pali maufumu awiri amene akulankhulidwa apa mu Mau a Mulungu. Umodzi ndi Ufumu wa Mulungu, wina ndi Ufumu wa Kumwamba. Ufumu wa Mulungu umabwera osati mwa kuonerera, uli mwa inu, ndipo ndi wangwiro, ndi wosadetsedwa. Kenako pali Ufumu wa Kumwamba umene ndi nyengo ya nthawi imene ikugwirizana ndi mibado ya mpingo; ndipo mkatikati mwa ufumu wa kumwamba, tirigu ndi namsongole zikukulira limodzi (Mateyu, chaputala 13) chifukwa ndi ufumu wa thupi, ndi chidzikodziko cha chipembedzo cha

chikhristu. Ufumu uwu wa kumwamba wafika kumapeto kwa Mkwatibwi; ndi chimene vesi 6 ikutionetsera ife.

Mngelo uyu anaima ndi kulumbira..., tsopano ine ndikufuna inu kuti muone, Iye akulumbira pa wamkulumkulu woposa Iyemwini. Pamene Mulungu anapanga pangano ndi Abrahamu, Iye analumbira pa Iye yekha, chifukwa Iye sakanatha kulumbira pa wina aliyense wamkulu. Koma apa pali mngelo, amene ndi Khristu mu maonekedwe auzimu kubwera ku dziko ndipo akukweza dzanja lake kumwamba ndi kulumbira pa Iye wamuyaya amene analankhula ndi Yohane kusindikiza bukhu. Iye analumbira kuti nyengo iyi kulibenso, ndiye kenako Iye akulozanso kuchimene chachitika mu nthawi yathu. Vesi 7 akuti, *“Komatu m’masiku a MAU a mngelo wachisanu ndi chiwiri m’mene iye adzayamba kuomba, pamenepo padzatsirizika chinsinsi cha Mulungu, monga analalikira kwa akapolo ake aneneri.”* **Kumeneko ndi kutsegulanso.**

Tsopano taonani, pamene mngelo wauzimu wachisanu ndi chiwiri uyu aomba, iye awomba molunjika kudzera kwa William Branham, mngelo wachisanu ndi chiwiri, nyenyezi, wam’thenga wapansi pano, ndipo pamene awomba, chinsinsi, ndipo ine ndikufuna inu muone Mau awa – mauwa ndi chimodzi **“chinsinsi;”** osati zinsinsi zonse za mu Baibulo. Ndi chinsinsi ichi cholankhulidwa ku Chivumbulutso, chaputala 1:20 chimene chikuchita ndi choikapo nyali zisanu ndi ziwiri, mibado isanu ndi iwiri ndi nyenyezi zisanu ndi ziwiri. Iye anati nyengo iyi idzafika kumapeto, (imeneyo ndi mibado ya mpingo) ndipo kwa Mkwatibwi, zinsinsi zonse zimene zikukhudzana ndi nyengo ya nthawi iyi zaululidwa ndi uthenga wamngelo wachisanu ndi chiwiri.

Tsopano ife tikuyenera kusuntha kupita ku uthenga umene siukugwirizana ndi nthawi ya ufumu wa kumwamba, **chifukwa zonsezi sizinamveke mu tsiku la Paulo.** Mu masiku a Paulo pano pa dziko lapansi, inu mukanati mulalikire mibado isanu ndi iwiri, Mizimu isanu ndi iwiri, angelo asanu ndi awiri, nyenyezi zisanu ndi ziwiri, kapena mabingu asanu ndi awiri..., Paulo akanatha kukuyang’anani inu ndikunena ‘Kodi munthu uyu wachokera kuti?’ Panalibe chirichonse ngati chimenecho mu Mau, chifukwa anali Yesu Khristu mu mpingo. Akanakhala munthu wachilendo ku uthenga wa Paulo. Izi ndi zinthu zimene tadutsamo kupyola mu nthawi pamene mpingo wadutsa mu mibado isanu ndi iwiri, ndipo Mulungu akuzionetsera izo kwa Mkwatibwi wa Khristu. Ife tikuona Mwanawankhosa amene akupita ndi kukatenga bukhu. Tikuona Mwanawankhosa ali ndi maso asanu ndi awiri (chimene ndi nyenyezi amithenga apansipano asanu ndi awiri), pa Mwanawankhosa wamagazi. Tsopano tikudziwa kuti icho chikuimirira Yesu ndi chimene Iye anachita pa Kavale, ndi m’mene zinakhala mu nthawi ya nyengo ya mibado ya mpingo kapena m’bado wa ufumu wa kumwamba. Taonani ichi..., Yesu Khristu analibe maso asanu ndi awiri ndi nyanga zisanu ndi ziwiri, ndipo inu mukanapita kumwamba usiku uno, inu simukanatha kuona cholengedwa cha mtundu umenewo. Mulungu anamulora Yohane kuona masomphenya kuti akathe kupanga mfundo apa.

Zinthu zonse izi zimene ine ndikulankhula kwa inu zokhudza **“zisanu ndi ziwiri”** zikhoza kukhala chilankhulo chachilendo ku mpingo woyamba. Inu musaphonye mfundo imeneyi. Zinthu zonsezi zimene ndikulankhula apa zikanatha kukhala chilankhulo chachilendo ku mpingo woyamba, ndipo kulankhula za mngelo wachisanu ndi chiwiri kubwera, Paulo akanatha kunena kuti “Iwe ukulankhula chiyani?” Iwe ukanati ulankhule chinachake za Martin Lutera ndi mngelo wachisanu, Paulo akanatha kunena, “Ine sindikudziwa zimene ukulankhula.” Chifukwa sizimadziwika mu mpingo woyamba; ndipo njira yokhayo zingadziwikire kwa ife pamene tikupanga maimidwe otsiriza awa kuno ku nthawi yotsiriza ndi mfundo ya mu mbiri..., kuonetsera njira imene Mulungu anabweretsera mpingo kudutsa ndipo ndizoti zikhale monga choncho. Zikuyenera kusiyidwa choncho. Tsopano ndikutha kuona chifukwa chimene ine ndinali ndi maloto a nyumba yowala ndipo kuwala kumene kunali kumeneko kunali mu nthawi yoyamba. Mu maloto, ine ndimatuluka kudzera

mu chitseko cha mwala, ndipo ndinati “Ine sindidzabweranso kuno.” Chifukwa chiyani? **Chifukwa Paulo sanakhaleko kumeneko...**, tsopano inu musaphonye mfundo imeneyo, chifukwa iyi ndi imodzi mwa mfundo zofunika kwambiri-----.

Zinthu zambiri zimene ife timalalikira, monga zikugwirizana ndi njira imene mpingo unabwerera, ife titangoti tinyamulidwe ndi kuikidwa mu mpingo wapachiyambi iwo akhoza kunena, “Muchotseni uyu muno.” Iwo akanatha kunena, “Muchotseni uyu,” chifukwa iwo anali nacho chinthu chimodzi cholalikira ndipo chinali Khristu. Iwo amakhala moyo umodzi ndipo unali Khristu. Iwo anali ndi chikhulupiriro cha mwana wa Mulungu, ndipo Paulo anachitcha chikhazikitso, sikulingalira kwinakwake, koma chikhazikitso. Ndi chikhazikitso cha uzimu, koma ndithu icho ndi chikhazikitso. Iye wapereka kwa yense wa ife muyeso wa chikhulupiriro. Paulo analalikira Mau a Mulungu kwa anthu ake mu tsiku lake; ndipo iye anati, “Chikhulupiriro chanu chikule mochuluka.” Apa ndi pamene ife tiri usiku uno, pamene Mulungu adzatipatsa ife chinachake kupangitsa chikhulupiriro chathu kukula mochuluka.

Kotero mngelo wachisanu ndi chiwiri anabwera ndi kuulura “chinsinsi” ndi kuchitsiriza icho, koma iye anati, **“Bwererani ku chiyambi, bwererani ku chimene Paulo analalikira.”** Inu mukatero, ndipo inu mukadzuka ndikulalikira mibado isanu ndi iwiri ya mpingo, **inu simukulalikira chimene Paulo analalikira.** Inu mukalalikira m’bado wa ufumu wa kumwamba, inu simukulalikira chimene Paulo analalikira. Inu mukalalikira nyenyezi zisanu ndi ziwiri, inu simukulalikira chimene Paulo analalikira. Inu mukalalikira Yesu Khristu Wamsembe Wamkulu mu m’bado wa mpingo, inu simukulalikira chimene Paulo analalikira. Inu mukalalikira mabingu asanu ndi awiri, inu simukulalikira chimene Paulo analalikira. Zonse izi sizingakhale pa maziko a Paulo. Ndi chinthunzi thunzi chosaoneka –**“Mabingu asanu ndi awiri – chinthunzi chosaoneka.”** Chinali chinthunzi cha chinachake chimene chinali kunja kwa uthenga wa Paulo. Izi ndi zochitika zimene zinachitika pamene mpingo unali kunja kwa dzikolakwawo. Zinthu zonsezi – “chinsinsi chimenecho” chinaikidwa kumeneko, kuti pamene nthawi ifika, Mulungu akhoza kutumiza mneneri wam’thenga wa ku Chipangano Chakale ndipo iye akanadzaulura chinsinsi chimenecho chimene chinaikidwa kumeneko, ndiye Mulungu akanamuchotsa iye padziko.

Kenako tikuona kutsatira mapazi a M’bale Branham panali M’bale Raymond Jackson (Jeffersonville, Indiana USA). Ife tikudziwa kuti Ayuda ndi Amitundu anakhala mbali ndi mbali mu mibado ya mpingo, ndipo pamene chisindikizo chachisanu chinaululidwa, zinapanga ife kudziwa kuti Ayuda ndi abale, ndi chimene iwo anali mu mpingo woyamba. Tsopano taonani; pakati pathu ife ndife abale ndi alongo koma zikafika pa Khristu, Ayuda ndi Abale Ake ndipo Amitundu ndi Mkwatibwi Wake. Pali kusiyana kwakukulu pakati pa abale ndi mkwatibwi. Ine ndimatenga mkazi wanga pamodzi nane usiku uliwonse, koma ine sinditenga m’bale wanga. Ine ndimakonda kukisa mkazi wanga pafupipafupi, koma m’bale wanga atayerekeza kundikisa kapena kundiyandikirira pa nkhani imeneyo, ine ndikhoza mwa mtheradi kunena, “Hey, vuto lako ndi chiyani? Iwe uli ndi mzimu wina wolakwika mwa iwe kapena chinachake.” Chabwino, Ayuda, iwo ndi Abale, ndipo Mulungu anatumiza Raymond Jackson kutidziwitsa ife malo awo mu dongosolo la Mulungu la nthawi ino yotsiriza.

M’bado wa ufumu wakumwamba usanayambe, panali Paulo, ndipo Mulungu anali atamudzutsa iye kukalalikira kwa Amitundu; ndipo kunalinsu Petro, amene Mulungu anamudzutsa kukalalikira kwa Ayuda. (Agalatiya, chaputala 2) Baibulo likuti, “Pamene Paulo anali ndi uthenga wa kwa osadulidwa; Petro anali ndi uthenga kwa odulidwa. Wamphamvu yemweyo amene anachita mwa Petro kwa Ayuda analinsu yemweyo wamphamvu kwa Paulo kwa Amitundu.” Kotero zinthu izi zikutipatsa ife kachitidwe ka m’mene zinachitikira, ndipo tikupeza kuti mu nthawi iyi M’bale Branham atachoka pa dziko, apo panabwera munthu dzina lake Raymond Jackson, mtumwi, ndipo Iye anatirora ife kudziwa pamene Ayuda ali mu dongosolo la Mulungu, chifukwa ndi zofunika kwambiri Mkwatibwi kudziwa Abale ake. Khristu anatidziwitsa ife Abale ake pogwiritsa ntchito

utumiki wa M'bale Jackson, ndipo pano Khristu akudziwitsa ife Atate pamene mau a ulamuliro akulankhula. Tsopano ife sikuti tikungodziwa kuti Mkwatibwi ndi ndani, ife tikudziwa chimene Abale ali ndipo tikudziwa chimene Atate athu ali. Mulungu ndi Mzimu ndipo iwo wompembedza Iye ampembedze mu Mzimu ndi mu choonadi. Ndipo nthawi yonseyi pakhalala pali Mulungu m'modzi, chikhulupiriro chimodzi, Ambuye m'modzi, ndi Mulungu kukonzekeretsa mpingo kuti uchoke pano, monga izi zadziwika kwa ife.

Tsopano Bukhu limenelo (Mau olankhulidwa) linali lotseguka ku mpingo wapachiyambi, koma tsopano watsegukanso kwa Mkwatibwi pano mu nthawi yotsiriza. Ine ndikufuna inu muone pamene ife tikufika ku vesi la chisanu ndi chitatu la Chivumbulutso, chaputala chakhumi. Kumbukirani ichi, mibado ya mpingo yatha, ndipo Khristu wabweranso kudziko mu maonekedwe a Mngelo Wamkulu tsopano. Ife tabwereranso ku chiyambi. Usiku wathawu ife tinaonetsera utumiki umene ukutiyeembekezera ife pamene tifika ku dzikolakwathu. Abale ndi Alongo ngati chikhulupiriro chanu chingadzuke, ife tiri ku dzikolakwathu. Ife tafika kumene Khristu Yesu ali pakati pathu, ndipo ife sitiri omangika ndi zolakwa ndi zolephera kapena zopambana za mu mibado ya mpingo. Khristu amene tiri naye ndi yemweyo amene iwo anali naye, ndipo kabukhu kakang'ono kaikidwa mu manja athu tsopano ndipo Iye akuti, "Pitani patsogolo, tengani dzikolo."

Taonani pamene tikuwerenga vesi 8; akuti, "Ndipo mau "tsopano taonani mau a ulamuliro..., ndi "mau" omwewo kuchokera kumwamba amene analankhula ku vesi 4 ndi kunena , "Sindikiza chimene mabingu alankhula. Sindikiza bukhu ndipo ulisiye iro losindikizidwa, mpakana mngelo wachisanu atabwera ndipo iye adzatsiriza (kapena kuulura) chinsinsi ichi cha nyengo ya nthawi ya ufumu wa kumwamba. Kenako ife tikuona mu vesi 8; pali mau a ulamuliro kulankhulanso..., Mulungu amene analankhula kale mbuyomu tsopano akulankhulanso. Pamene Mulungu akulankhulanso, ine ndikufuna ndisiyanitse chinachake pakati pa Mulungu ndi Mwanawake Yesu.

**Pamene Yesu anali pano, zonse za Mulungu sizinali pano. Pamene Yesu anabadwa, winawake anandiuza ine kuti anali Mulungu ali mu khola. Chabwino awo anali Mau kusandulika thupi ndipo Mau gawo la Mulungu, koma Iye amayenera kukhala chinachake, chifukwa pamene amafuna kumupha Yesu, Mulungu analankhula ndi Yosefe ndipo anati, "Tenga mwana wang'ono uyu upite naye ku Aigupto chifukwa akufunafuna kutenga moyo Wake." Mulungu amayenera kusamalira Iye ndikumusunga Iye pabwino, mpakana nthawi imene Iye angakhale mwa Iye; kenako zikatha izi, Yesu anayamba kugwira ntchito. Iye anati pamene amaukitsa akufa, "Si ine amene akuchita ntchito izi, koma Atate amene akhala mwa ine." Izo sizinapangitse thupi kukhala Atate, izo sizinapangitse munthu kukhala Atate, koma zinapanga Mzimu umene unali mwa Iye, Atate.**

Ku Chipangano Chakale monga ife tikutsatira nkhaniyo ya chiombolo, ife tikupeza kuti Mulungu analora mwanawankhosa kufa m'malo mwathu. Wamsembe amatha kuika mwazi pa guwa chifukwa cha machimo onse awo komanso a wanthu, ndipo amayenera kuzichita chaka chirichonse. Koma mzimu wa mwanawankhosa sumatha kubwera pa okhulupirira, chifukwa unali wosiyana ndi mzimu wa munthu. Ndi chifukwa chake Yesu anasandulika mzimu wa moyo kuti ife tikakhale monga iye ali, mu kakhaliidwe kameneko.

Ku Yesaya 53, pamene Yesu anapachikidwa pa mtanda, Baibulo likuti, "Iye anapereka moyo Wake ndi kufa," osati Mzimu Wake okha koma moyo Wake, kutanthauza kuti umunthu Wake. Moyoyo wa Khristu unatsanulidwa, ndipo tsopano Mulungu anali atapeza njira yodzilumikizira Iyemwini ndi banja la munthu. Inde, Iye anasandulika m'modzi wa ife kupyolera mwa Khristu. Kotero pamene Khristu amafa, Iye anafuula ndi mau akulu; ndipo Iye anapereka moyo umenewo (mzimu)/mzimu umene unali wolumikizidwa ndi Mulungu (Mzimu wa Muyaya). Izi zinabweretsa Mulungu ndi Khristu palimodzi mu Mzimu (Mzimu Woyera), umene ukanatha kukhala mwa munthu, kupanga Yohane 14:20 ndi 23 kukhala

wamoyo kwa ife. *“Tsiku lomwelo mudzazindikira kuti ndiri mwa Atate wanga, ndi inu mwa Ine, ndi Ine mwa Inu. (Yohane 14:20) “Yesu anayankha nati kwa iye, Ngati wina akonda Ine, adzasunga mau anga; ndipo Atate wanga adzamkonda, ndipo **IFE tidzadza kwa iye, ndipo tidzayesa kwa iye mokhalamo.**” (Yohane 14:23)* Osati monga Mulungu, Mzimu wamuyaya unaliri Yesu asanabadwe, koma monga anali atabwera mwa Khristu ndipo anasandulika m’modzi ndi Iye pa nthawi imene Yohane amamubatiza; ndi chimene Mau akulankhula, *“Ife tidzadza ndipo tidzayesa mwa iwe mokhalamo.”* Tsopano, mnzanga ndi Mzimu Woyera, ndipo ndi chimene chinabwera kwa okhulupirira. Ndi chimene analandira pa phwando la Chiyuda pa tsiku la Pentekosite. Ndi chimene analandira ku nyumba ya Koneliyo, pamene khomo linatseguka kwa Amitundu. Ndi chimene chinatsogolera mpingo, Mzimu Woyera, Khristu mu maonekedwe a uzimu, Mau odzozedwa. Tsopano kuno ku Chivumbulutso, chaputala cha khumi, ife tikuona Mzimu womwewo (Khristu) kubwera mu maonekedwe a Mngelo Wamkulu. Tsopano bukhu limene linali lotseguka ku mpingo woyamba ndipo linasindikizidwa pa nthawi imene mpingo woyamba unagwa ndirotsegukanso kwa anthu a mu nthawi yotsiriza, pamene mau a ulamuliro akulankhula kuchokera kumwamba.

Tsopano ine ndikufuna inu mudziwe kuti pamene mau awa akulankhula – amaika chirichonse m’ malo ake ndipo palibe chirichonse pa dziko chimene chingakhudze chimene Iye wachilamulira; chirichonse chimene Iye wachilamulira ndi kuchiika, palibe mwa njira iriyonse chimene chingalepheretse. Ine ndinali ndi nthenda ya mtima mu 2003, koma lero ndiri wamphamvu mochuluka kawiri. Mulungu anandipatsa ine maloto pamene ndinachoka mu chipinda chosungira odwala ku chipatala chimenecho. Iwo samadziwa kuti ndikhala ndi moyo kapena ndifa, koma pamene ndinafika kunyumba, Mulungu anandipatsa ine maloto. (Ine ndinali kupita kumalo ngati ku Alaska USA), ndipo kunali nam’mondwe, chimphepo chachikulu, ndipo wina anandipatsa ine masuti asanu a zovala ndi chakudya china. Zinali ngati zovala zimene anthu othamanga mu chifunga amavala. Ndipo zinalankhulidwa kwa ine, *“Ine ndikufuna iwe ukankhe malire. Tenga chakudya, tenga chovala, ine ndikufuna iwe ukankhe chifukwa cha iwo amene akukutsatira iwe.”* Kotero ine ndinayamba kuyenda mu chimphepo chochititsa khungu, nditatenga chakudya ndi chovala. Ngakhale kuti sindinakhalepo chonchi kale, zikuoneka ngati ine ndimadziwa kwenikweni kumene ine ndimapita ndi chimene ndimakachita.

Chabwino abale ndi alongo ndiloreni ine ndikuuzeni chinachake, Mulungu yemweyo akulankhula lero, Mulungu wa Kumwamba, Iye analamulira chinachake ndipo pamene Iye alamulira chinachake, palibe amene angachilepheretse icho. Dzuwa lakhala likutuluka ndi kulowa kwa zaka mamiriyoni, ndipo mamiriyoni a zaka kuchokera pano idzakhalabe ikuchita zomwezo. Mu nthawi ya mileniamu idzakhalabe ikuchita zomwezo, chifukwa Mulungu wailamulira iro. Tsopano pamene Mulungu alamulira chinachake, ndi pokhapo ndipo ndi pokhapo pamene inu mukhoza kuchita icho. Mau akulu a ulamuliro amene analankhula mu masiku a Yohane ndi kunena kuti, *“Sindikiza chimene mabingu asanu ndi awiri analankhula. Sindikiza bukhu, sindikiza chimene chidzachtike ku mibado ya mpingo isanu ndi iwiri.”* Koma tsopano zinthu izi zonse zauluridwa kwa ife pano mu nthawi yotsiriza.

Tsopano Chivumbulutso 10:8, *“Ndipo mau ndinawamva ochokera kumwamba, tsopano taonani, osati kulankhula padziko, **“ndipo mau ndinawamva ochokera kumwamba, analankhulanso nane,”*** iyi ndi nthawi yachiwiri mau awa a ulamuliro akulankhula. Nthawi yoyamba Mulungu akulankhula ndi Yohane, Iye anamuonetsera iye mibado ya mpingo ndi kumuuzza iye kuti asindikize, ndipo anamuuzanso Yohane nthawi (kapena m’mene) Iye adzatsegulanso bukhu. Koma pamene *“chinsinsi”* ichi chidzatsirizidwa, ndipo ufumu wakumwamba udzakhala utatha..., ndipo mau ochokera kumwamba akulankhulanso kachiwiri, *“Ndipo anati, Pita ukatenge kabukhu kakang’ono kamene kali kotsegula”* tsopano ife talamulidwa kupita kwa Mngelo Wamkulu ndi kukatenga bukhu.

Tsopano apa pali chinthu chofunika...., kwinakwake Mulungu amalumikiza ulamuliro umenewo mu mzere. Usiku watha ife tinazibweretsamo izo, m'mene mau a Mulungu kwa Mkwatibwi amabwerera kupyolera mu utumiki umene Iye anauika kuti ugwire ntchito pamene ife tibwerera kudziko; uwu ndi utumiki wa, atumwi, aneneri, alaliki, abusa ndi aphunzitsi." Choyamba chikuyenera kukhala kumverera komweko mu mtima mwanu ndipo ine ndalankhula ndi osiyanasiyana, aliyense ali nako kumverera komweko mu mtima mwake, *pali chinachake chatsala pang'ono kuchitika, Haleluya pali chinachake chatsala pang'ono kuchitika*. Ndi mau omwewo kulankhula mwa inu; kumverera kumene muli nako.., ndi nthawi yoti mulandire zochuluka kusiyana ndi zimene tiri nazo. Ndi nthawi yochita mochuluka kusiyana ndi m'mene tikuchitira.

Kodi kabukhu kakang'ono ndi chiyani? Ndi Mau osalembedwa a Khristu. Ine ndikufuna ndibweretsemo mfundo iyi ndisanapitirire: Ngati Mngelo Wamkulu ali Mngelo Wauzimu, Iye sakubweretsa bukhu logwirika. Tsopano kodi mwazigwira zimenezo? Mungalore ndilankhulenso kuti ndifotokoze? Mngelo Wamkulu ndi Mzimu ndipo Iye akubweretsa bukhu, lotsegula. Bukhu lotsegula iri si Baibulo. Baibulo iri – Mau wolembedwa ndi mtengo wa chidziwitso, koma Mtengo wa Moyo umamera kutuluka mu iro; chifukwa Baibulo likuti, "Lemba limapha koma Mzimu ndiye apatsa moyo." Iye sakubweretsanso Baibulo iri, chifukwa ife tinali nalo nthawi yonse. Iye akungobweretsa Mzimu wa Mau ndi kutilamulira ife kuwapanga iwo kukhala amoyo mu nthawi iyi yotsiriza. Tsopano inu taonani, "Pitani katengeni kabukhu kakang'ono kamene kali kotseguka," ndi kotseguka kwa ife pano nthawi ino. Paulo anati, "Ndi Khristu mwa inu, chiyembekezo cha ulemerero." Iye anati, "Inu ndinu mamembala a thupi la Khristu." Iye anzilankhula mu njira zosiyanasiyana, koma nkhani ndi yakuti, pamene ife tiona Mkwatibwi, ife timaona Khristu. Iye tikuchitira umboni ukwati wa Khristu ndi Mkwatibwi Wake, ngakhale pamene tikulankhula.

Mu mpingo woyamba, mpingo usanagwe, Paulo anapalitsa ubwenzi mpingo kwa Khristu (2 Akorinto, 11:2). Iye anati, "*Ine ndakupalitsani inu ubwenzi kwa mwamuna m'modzi, kuti ndikalangize inu ngati namwali woyera mtima kwa Khristu. Koma ndiopa, kuti pena m'monga njoka inanyenga Heva ndi kuchenjerera kwake, maganizo anu angaipidwe kusiyana nako kuona mtima ndi **KUDZICHEPETA** ziri mwa Khristu.*" Chinjoka chomwecho chimene chinanyenga Heva, chinanyenganso mpingo woyamba, chifukwa Paulo asanachoke iye anati, "Pali anthu pakati panu tsopano, ndipo ine ndikangochoka, iwo adzadzuka ndikudzitengera okha ophunzira." Mulungu anawatengera atumwi kumudzi, ndipo mpingo unapita mu m'bado wa m'dima. Bukhu linali losindikizidwa mu 96 AD, monga Mulungu anamulangizira Yohane kuti alisindikize, ndipo linakhala losindikizidwa kwa zaka zikwi ziwiri, ndilotchedwa (mibado ya mpingo). Monga m'mene Paulo analumikizitsa mpingo; pali utumiki umene ukumukwatitsa iye.

Inde, pali ukwati umene ukuchitika mu tsiku iri lotsiriza, ndipo Iye anati ife tidzasandulika fupa la fupa Lake ndi thupi la thupi Lake, ndipo pano ife tasandulika Mzimu wa Mzimu Wake. Mau a Mulungu amatiphunzitsa ife ku chaputala cha 19, ku bukhu la Chivumbulutso, kuti Mkwatibwi wadzikonzekera yekha ndipo kwa kunapatsidwa kuti avale bafuta wonyezimira, chimene ndi chilungamo cha oyeramtima..., **ndipo chilungamo cha Mulungu kubwera kwa inu ndi uthenga wotsiriza Mkwatibwi uyu adzaumva**. Chidzafika ndipo sizidzakhala mwa ntchito zabwino! Abale athu amene ndi Ayuda (Aroma, chaputala 9, 10 ndi 11, zikuchita ndi zimenezo mu machaputala atatu kumeneko), akufotokoza kuti amapita kusaka chilungamo mwa ntchito, ndipo pochita zimenezo uko ndi kukana chilungamo cha Mulungu. Ngati inu mukuganiza kuti mukhoza kuchita chinthu chaching'ono chimodzi kuti mukhale olungama, uko ndi kulankhula kuti Iye si okhoza kundipanga ine wolungama, koma pamene inu mukhala mwa Iye, inu mumakhala olungama monga Iye ali.

Mu chaputala cha 5 cha 2 Akorinto; Paulo akulankhula kumeneko ndi kunena kuti ife ndife oimirira Khristu, koma vesi lotsiriza likuti, "Mulungu wamupanga Khristu kukhala

tchimo chifukwa cha inu ndi ine, ndipo Iye wakupangani inu chilungamo cha Mulungu mwa Khristu Yesu.” Anthu ena amanena, “Chabwino ine ndimakhulupirira Khristu anafera machimo anga, koma imeneyo ndi gawo chabe la vesi ndipo ingokufikitsani inu ku kagawo kena ka njira. Inu mukuyenera kukhulupirira kuti inu ndi chilungamo chenicheni cha Khristu. Iye anatenga machimo anu ndi kukupatsani inu chilungamo chake, ndipo tinachita malonda opambana kwambiri. Kotero ine ndiri wolungama monga Yesu ali, osati mwa ntchito yanga iriyonse kapena chirichonse, koma chifukwa choti ndiri mwa Iye ndipo ndafa ndipo moyo wanga wabisika ndi Khristu mwa Mulungu, ndipo m’dierekezi sangandipeze.

Inde, ndi njira yokhayo inu mungakhalire ndi chikhulupiriro, chifukwa tchimo limapha chikhulupiriro. **Paulo analikira chilungamo cha Mulungu ndipo chikhulupiriro cha anthu chinakula mochuluka.** Inu muli nawo mwai usiku uno oti chikhulupiriro chanu chikakule, ndipo chikhulupiriro chanu chikuyenera kukula. Koma sichidzakula pokhapokha mutazindikira “Ine ndine woyenera,” osati pa chifukwa cha chirichonse chomwe ndachita, koma kuti anandipanga ine kukhala woyenera. Iye anafa pa mtanda chifukwa cha ine ndipo chilungamo chake chonse, Iye anandipatsa ine! Mulungu sangathe kuona machimo anga, chifukwa Iye amaona Khristu ndipo saona tchimo. Iye amene abadwa mwa Mulungu sachimwa, chifukwa mbewu imakhalabe mwa iye; ndipo izi zikuchita ndi wamkatiyo, pansu mkati mwa mkati. Iye sangandiimbe ine mlandu wa tchimo. Mukudziwa chifukwa chake? Pali wina amene adzaima ndi kuimirira ine. Ngati m’dierekezi angayesere kuika tchimo pa inu, Khristu akuti, “AYI, inu mukuyenera kuika pa ine, chifukwa iye ali mwa Ine.”

Tsopano ife tikulalikira uthenga uwu kwa anthu onse, mafuko onse ndi manenedwe, ndi mafumu (kapena maufumu). Mulungu wakonza njira, Iye akuchita zimenezo, inu mukukhala moyo m’masiku a Baibulo; malemba akukwaniritsidwa. M’bale ife tiri ndi chinachake chochitika posachedwapa; ife tiri ndi chinachake chimene chidzatitulutsa pano. Ife tidzayenda mtunda wautali pamene mapiko a mphungu adzatitenga ife, ndipo kenako tidzapitirira, chifukwa ife tiri mwa Khristu ndipo ndife olungama monga Khristu ali wolungama. Baibulo limatiphunzitsa ife kuti chimwemwe cha Khristu ndiye mphamvu zathu. Anthu ambiri amasandulika a khristu wofoka, koma ndikuuzani inu kuti ino si nthawi yokhala wofooka. Baibulo likuta, “Lorani iye amene ali wofooka anene ndiri wamphamvu.” Lankhulani mau akuluakulu, “Ine sindiri wofooka, ine ndiri wamphamvu, ine ndiribe chikhulupiriro chaching’ono, ine ndiri ndi chikhulupiriro chambiri, osati ndiri ndi chikhulupiriro chochepa, Mulungu anandipatsa ine muyeso wa chikhulupiriro kuyamba ndi kuyamba, koma ine ndakhala ndikuchilora icho kukula.” Chikhulupiriro chimadza pakumva ndipo kumva mau wouluridwa a munthawi imene ife tikukhalamo.

Inu mukhoza kuwerenga lemba, ndipo inu mukuwerenga za mtengo wa chidziwitso. Ndi zabwino pokhapokha ngati Mtengo wa Moyo ukumera kuchokera mu iro. Mtengo wa Moyo ndi kumene moyo uli, ndipo ndi Mau a Uzimu..., ndipo ndi chimene Yesu akubweretsa kwa ife kuchokera ku Paradaizo; ndi kabukhu kakang’ono ka ku Chivumbulutso, chaputala chakhumi.

Chabwino ndiloreni ine ndikuuzeni chinachake..., “Mu masiku a Baibulo bukhu linali lotseguka, Mtengo wa Moyo unali wopezeka, ndipo unali pakatikati pa Paradaizo wa Mulungu.” Ahebri, chaputala 12; Paulo anati, “Inu mwafika ku Yerusalemu Watsopano, inu mwafika ku khamu la angelo kumwamba, inu mwafika ku kumene mizimu ya anthu olungama imakhala yangwiro, inu mwafika kwa Yesu Khristu, inu mwafika ku makamu ochuluka a angelo, inu mukukhala palimodzi ndi Khristu Yesu m’ malo a mwambamwamba.” Bukhu ndi lotseguka kwa ife tsopano, Mau a Uzimu amenewo amene Iye (Khristu) anabweretsa.

Pamene mpingo unagwa, Mulungu anati, “Sindikiza kabukhu kakang’ono.” Iye anatenga kumvetisa (Mzimu) wa icho (Moyo wa icho), ndi kusiya lemba la Mau, ndipo ife takhala tiri ndi lemba la Mau. Mpingo wa dziko wamanga masukulu, iwo amanga ma seminare mu

nthawi ya ufumu wa kumwamba. Mulungu anazilora zimenezo, monga m'mene Iye anamulorera Israeli ku Chipangano Chakale kupereka msembe mwanawankhosa, ndipo Mulungu anazivomereza izo ngati chilungamo; chifukwa iwo anali atagwa ku chiyero cha Mau. Iye anatenga mzimu wa Mau ndi kusindikiza bukhu, koma tsopano Iye akubweretsanso Mzimu wa Mau ndi kuika pomwepo pa bukhu. Ziri monga zinaliri mu munda wa Edeni. Ndiloreni ndinene ichi kuti mukathe kumvetsa chimene ndikulankhula.

M'munda mwa Edeni pamene munthu anagwa, Mulungu anachotsa Edeni; Iye anathamangitsa munthu mu Edeni. Koma mukudziwa kuti iye sanachoke mwathupi ngakhale phazi limodzi? Unali Mtengo wa Moyo umene anauchotsa, amene anali Edeni wa uzimu. Koteropamene Iye anachotsa Mtengo wa Moyo, Iye sanatengapo mchenga ngakhale umodzi, Iye anangochotsa Mzimu wa Edeni ndikusiya dziko. Pamene mpingo unagwa, Mulungu sanachotse mau olembedwa, Iye sanachotse ngakhale limodzi la makalata a Paulo. Iye anangochotsa Mzimu pa Mau olembedwa ndipo ife tinakhala ndi moyo mwa Mau olembedwa kwa zaka zikwi ziwiri..., koma tsopano akubweretsanso Mzimu wa Mau ndi kuika iwo pa lembe la Mau. Ife tikuona Mtengo wa Moyo ukuyamba kumera pa Mau awa. Pali Mau otseguka kwa ife lero, bukhu ndi lotseguka m'bale, ndipo mau akulu a ulamuliro a Mulungu akuti, "PITA, katenge bukhu."

Tsopano taonani ichi mu vesi 9; Iye akumuuzza Yohane, "Pita katenge kabukhu kakang'ono," choyamba inu mukuyenera kukhala nako kumverera kumeneko, kodi inu muli nako kumverera kumeneko? Ine ndikanatha kukhalitsa pamenepo, koma ife tiribenso usiku wina kuno. Ife tikuyenera kutseka usiku uno. Vesi 9 akuti (ichi ndi chimene mukuyenera kuchita) inu simungachite icho pokhapokha mutamvetsa kuti mwauzidwa kuchita izo. Vesi 9 akuti, **Ndipo ndinapita kwa mngelo, ndipo ndinati kwa iye, Ndipatse kabukhu kakang'ono.** Kodi inu munganene usiku uno, ndipatseni kabukhu kakang'ono? Ndipatseni ichi chimene mpingo wa pachiyambi unali nacho; bukhu limene ndi lotseguka. Iye sanakupatseni inu bukhu lotsekedwa, koma Iye anakupatsani inu bukhu lotseguka. Choyamba mukuyenera kumva mau a ulamuliro akunena, (Pita katenge iro)! Izi zimakupatsani inu kulimbika, izi zimakupatsani inu chikhulupiriro, zimakupangani inu kudziwa kuti ndi nthawi yake, zimakupangani inu kudziwa kuti ndi nthawi yokatenga bukhu. Kenako inu mumayenda kupita kwa Mngelo Wamkulu, zimene zonse ziri mwa uzimu, inu mumayenda ndi kunena, "Ndipatseni kabukhu kakang'ono." "Ambuye ine ndiri wokonzeka kulalikira mwa Mzimu, ine ndiri wokonzeka kukhala chilungamo chimene chiri mwa Khristu Yesu, ine ndiri wokonzeka!" **Taonani ichi tsopano:** Inu simungathe kupita kwa mngelo amene ndi Khristu mu maonekedwe awa padziko, pokhapokha muli ndi chilungamo. Tchimo siringalowe pamenepo, ngati muli wothodwa ndi tchimo, chotsani iro tsopano; ngakhale pamene ndikulankhula. Inu munene, "Ambuye ine ndapanga zolakwitsa, koma tsopano ndikufuna bukhu. Mulungu, ndibiseni mwa Khristu mumene mulibe tchimo." Inu mukuyenera kufa kwa inu eni. Moyo wanga uli ndi chinthu chimodzi, ndipo ichi "ndi Mau." Ichi chimapereka ku moyo wanga cholinga, ichi chimandipatsa ine cholinga chokhalira moyo, anthu amene alibe cholinga chokhalira moyo amakhala anthu omvetsa chisoni. Pali anthu ena a mu mpingo amene alibe cholinga cha moyo wawo..., koma ife tiri nacho cholinga, ife tiri ndi mphamvu, ife tiri ndi bukhu, ife tiri ndi Yesu Khristu ndipo ife tiri naye Iye njira yomweyo mpingo woyamba anali naye Iye. Ife tamva mau a ulamuliro akulankhula pita katenge bukhu ndipo tikupita kwa Iye ndi kuyamba kulankhula.

Ine ndikuganiza za Paulo pamene iye anali pa njira yaku Damasiko pamene kuwala kwakukulu kunamugwetsa iye pansu, ndipo Ambuye anamulankhula iye nati, "Pita ku mzinda mu khwalala lotchedwa Lowongoka, ndipo udzauzidwa zochita." Ndipo pamene iye anafika kumeneko, panafika mkulu wina otchedwa Anania. Ambuye anali atalankhula kale ndi Anania ndikumuuza iye za Saulo (Paulo), ndipo Anania analankhula ndi Ambuye. Iye anati, "Ambuye, ine ndamva za munthu ameneyu, ndikuti iyeyu waononga kwambiri oyeramtima,

ndi zoonza kuti ichi ndi chimene mukufuna kuchita?” Ambuye anati, “Pita.” Ndipo Anania anapita ndi kunena, “Saulo, Ambuye, ngakhale Yesu amene anaonekera kwa iwe pa njira, Iye anakuuza iwe kuti ubwere kuno,” ndipo Anania anayamba kumuuzza iye za Yesu Khristu. Ndipo panali Petro pamwamba pa nyumba, iye anati, “Ambuye ndi zoonza kuti inu mukufuna ine ndipite kwa Amitundu?” Iye anati, “Pita! Usakaikire chirichonse.”

Ndi chimene vesi 9 la bukhu la Chivumbulutso, chaputala cha 10 chikulankhula, “Pita katenge kabukhu kakang’ono.” Kodi ungapite? Kodi ungapite – osakaikira chirichonse? Kodi mungamve mau, kodi mungamve lipenga likuomba; kodi mungamve Mau a munthawi ino? Ndiye zimakupatsani inu kulimbika. Choyambirira, mukuyenera kuzindikira kuti inu muli wangwiro monga Iye ali wangwiro, chifukwa inu simungatenge bukhu ndi kumayenda mokaika, kumakwawa ndi kumamupempha Iye. Ayi! Osapempha, mungomufunsa Iye. Pitani mukatenge bukhu ndi kunena, “Zikomo inu, Yesu.” Iye siopempha, ife ndife olowa naye pamodzi Mulungu pamodzi ndi Khristu, ife ndife gawo la Iye ndipo anatipanga ife kukhala gawo la Mau. Paulo atayang’ana gululo iye anati, “Inu ndinu akalata wolembedwa, inu ndinu Mau, inu ndinu uthenga umene ine ndikulalikirira, inu ndinu mphamvu ya Mulungu ndipo mwasandulika chilungamo cha Yesu Khristu.” Chifukwa iye anasandulika tchimo chifukwa cha inu, inu mumasandulika chilungamo Chake. Kotero Yohane anapita ndikunena, “Ndipatseni kabukhu kakang’ono.” Ndi angati amene anganene zimenezo usiku uno? “Ndipatseni kabukhu kakang’ono?” Kodi mukukhulupirira kuti liripo kwa inu? Kodi mukukhulupirira kuti zisindikizo zachotsedwa? Mulungu watsiriza m’bado uyu wa tirigu ndi nansongole kukulira limodzi.

Tsopano pamene Mulungu akutisuntha ife ku vumbulutso lalikulu, nthawi zina Iye akuyenera kutengera atsogoleri akuluakulu kumudzi amene anali pakati pathu, ngakhale tiwayamikire motani, ngakhale tiwakonde motani, ngakhale tikonde ntchito imene iwo achita, inu mukuyenera kupitabe ndi vumbulutso, pozindikira kuti akanachitanso chimodzimodzi. Mukuona, inu mukadali pano, Khristu ali pano, Mau ali pano, Mzimu Woyera uli pano, mphamvu ya Mulungu iri pano, chikhulupiriro chiri pano ndipo akukuitanani inu kuti mudzuke kuti mukhale chinachake cha Iye mu nthawi yotsiriza iyi, chifukwa ife tiri kumapeto kwa m’bado. Kotero inu mumadzuka ndikunena, “Ndipatseni ine kabukhu kakang’ono.” Inu mukuyenera kudziwa kuti kalipo kwa inu. Ngati inu simukudziwa kuti kalipo, nanga inu mufunsa bwanji? Tamverani, Ine sindikuyesera kukhala wotsutsa, chifukwa sitikuyenera kutsutsa aliyense. Ine sindikuyenera kutsutsa wa Baptist, ine sindikuyenera kutsutsa wa Methodist, ine sindikuyenera kutsutsa wa Pentekosite, ine sindikuyenera kutsutsa wina aliyense, **chonse ine ndikuyenera kuchita ndi kulalikirira uthenga ndi chikondi ndipo Mulungu adzachita zotsatirazo**, ndipo iwo amene ndi woikidwa kuchiona icho, iwo adzafunsa kabukhu kakang’ono ndi kukatenga iro.

Pakhala pali iwo amene anabwera mbuyomu amene akuti chisindikizo chachisanu ndi chiwiri sichinamasulidwe, mabingu sanalankhule ndi zina zotero..., chabwino chimenecho chimapha chikhulupiriro chonse chimene inu mukhoza kukhala nacho kukatenga bukhu. Chifukwa poyambirira, inu mumaganiza kuti bukhu palibepo pano; kachiwiri, inu mumaganiza kuti mabingu sanalankhule. Chabwino iwo anaomba. Ngati inu mutafuna kuti mudziwe izo, iwo anaomba mu 96 A.D, ndipo anasindikizidwa nthawi imeneyo. Chinthu chokhacho Mulungu anachita mu tsiku iri kunali kutumiza angelo womwewo asanu ndi awiri amene analipo ku chiyambi cha mibado ya mpingo (Chivumbulutso, chaputala 1) ndi kuulula izo kwa wamthenga wa m’bado wa chisanu ndi chiwiri. Chimodzi mwa zinthu zofunika zimene zisindikizo zinachita kunali kutirozera ife mbuyo ku mfundo ya mu mbiri monga m’mene mpingo wayendera, kotero kuti tikadziwe pamene tikuima mu nthawi ino. Kotero tikuyenera kudziwa kuti zinthu izi ziri mbuyo mwathu. Tsopano ife tikuona bwinobwino kusiyana ndi kale. Kodi mukudziwa chifukwa ndinalankhula mu maloto aja “ Ine sindidzabweranso malo ano?” Chifukwa ine ndimabwera ndikumapereka ulemu ku kuwala

chaka ndi chaka, chaka chirichonse ndimabwera ndi kupereka ulemu kuchimene Mulungu wachita. Koma panalibenso mphamvu pamenepo, palibe mphamvu mu mbiri, palibe mphamvu mu mau olembedwa, pokhapokha ali odzozedwa ndi Mzimu Woyera. Chinthu chokhacho lemba la Mau likhoza kuchita ndi kupha... ndi Mzimu umene upatsa Moyo.

Tsopano tiyeni tipitirire ndi ichi. “Ndipatseni ine kabukhu kakang’ono,” Yohane ananena. Kodi mukumverera mu mtima mwanu kuti mukhoza kuyenda kupita kwa Yesu ndikunena, “Ndipatseni chimene Mpingo wapachiyambi unali nacho? Kodi mungachite zimenezo? Kodi muli nacho chikhulupiriro chochita zimenezo? Inu mukhoza kutero ngati inu mukudziwa kuti muli angwiro monga Yesu Khristu ali wangwiro, ndipo sindikulankhula za mtembo wanu. Ine sindikulankhula za zolephera za umunthu zimene timapanga pamene tikuyenda pa njira. Ine ndikulankhula za moyo wamkati umene wasindikizidwa ndi Mzimu Woyera mpakana tsiku la maomboledwe. Ife timaphunzira pamene tikupita tsiku ndi tsiku ndipo timakula. Koma wamkatiyo inu ndiwosindikizidwa ndi Mzimu Woyera mpakana tsiku la maomboledwe ndipo inu mwafa ndipo moyo wanu wabisika ndi Mulungu mwa Khristu, ndipo inu muli woyera monga Khristu chifukwa Iye anakupatsani inu chilungamo Chake. Tsopano inu mukukonzeka kukatenga bukhulo, chifukwa m’dierekezi ayesera kuponya chirichonse angathe kwa inu.

Ine ndimasala kudya kamodzi kwa masiku ambiri, ndikukhulupirira pafupifupi masiku makumi awiri ndi asanu pa nthawi iyi, koma ndimatha kukhala bwinobwino, kumamverera bwinobwino mwa Ambuye ndipo mwadzidzidzi m’dierekezi amatha kubweretsa zinthu zina mwinamwake zimene ine ndinachita kapena kulankhula chinachake mbuyomo, ndipo zikanatha kungopha chikhulupiriro changa. Ine ndimatha kukhudzidwa, pansi pa mzimu wanga mpakana kulephera kukweza mutu wanga. Kenako ine ndinali ndi maloto ndipo panali mpukutu wa makiyi amene amagwedezeka kutsogolo kwanga ndipo ndimafuna kuwafikira koma anali ma inchesi awiri patsogolo, ndimalephera kuwatenga. Mu maloto amenewa ine ndinali nditafa ndipo ndinakathera ku Gehena ndipo m’dierekeziyo anali kumeneko ndipo iye amaseka, iye amalumphu, zimakhala ngati anali pa zingwe kumalumphu mwamba ndi pansi, kamunthu kakang’ono ndithu. Iye amangolumphu ndi kumaseka ndipo kuseka kopsyetsa mtima kumene inu simunakumveko, ndipo zikhoza kupanga khungu lanu kuyenda, kukupangani inu kukhala okhumudwa, kukupangani inu kumverera “Ndingofa ine, ine ndichite chinachake, ine ndisakhale moyo, Ambuye.” Ndipo satana amaseka ndipo anatchula zinthu zitatu, “Iwe unachita ichi uli padziko lapansi, unachita ichi, ndipo unachita ichi, Ha ha ha ha ha ndipo tsopano ndakugwira”. Chabwino izo zinali zina mwa zinthu zimene zimabwera ku malingaliro anga ndi kumandisautsa. Kenako mwadzidzidzi kunali ngati pa siteji, ine ndinamva chitseko chikutseguka, mwadzidzi satana amalumphu, kumaseka, kunditsutsa ndikumandipanga ine kumverera ngati ndikufuna kufa ngati ndingathe, (koma sindimafa). Ine ndinayang’ana mozungulira ndipo apo panabwera Ambuye Yesu Khristu, ndipo anayenda kumbali yanga. Iye sanalankhule mau amodzi kwa ine. Ine ndinaona satana akuyamba kunjenjemera, iye anayamba kuzizidwa. Yesu anati “Inde satana, pa dziko iye anachita ichi, pa dziko anachita ichi, ndipo padziko anachita ichi.” Iye anadutsa mu zinthu zitatu zomwezo satana amanditsutsa ine; kenako Yesu anati, “Ine ndinafa pa mtanda ndipo ndinasamalira chirichonse cha izo (zinthu zimenezo)..., Ine ndinasamalira tchimo lililonse ndipo Iye ali wopanda tchimo, iye ali wopanda banga kwa ine”. Satana anayamba kutha, iye anasoweratu, kenako ine ndinadzuka.

Abale ndi alongo ine ndikukuuzani inu, machimo anu analipiridwa ndipo machimo anu apita. Ngati inu simukudziwa ndiyemwanjira ina kapena inzake zikhoza kutchinga chikhulupiriro chanu, inu mukuyenera kukhulupirira mpaka muyeso wina, inu mudzafika potchinga msewu. Koma apo pakubwera Khristu kutipatsa ife chinachake kutitulutsa ife kuno, kutisinthu ife mu kamphindi, mu kuthwanima kwa diso, chifukwa Wamphamvu zonse walamulirira izo. Ife tafika ku chinachake. Yesu Khristu ali pakati pathu, Iye ali pano

kukukwezani ndikutipangitsa ife kukhala palimodzi mu malo anwambamwamba kumene mudzadziwa kuti muli mwambamwamba ndipo mukhoza kunena, “satana choka.” Kodi mukukhulupirira izo? “Choka satana. Ine ndikuyenda ndi Yesu.” Satana akuti, “Inde, koma kumbukira chimene unanena ndi malingaliro woipa amene unali nawo?” Inu mukuti, “Inde satana ine ndikukumbukira zonse izo, koma Yesu Khristu anandipatsa ine chilungamo chake chenicheni. Iye anatenga machimo anga ndikundipatsa ine chilungamo Chake ndipo moyo wanga wafa ndipo ine ndabisidwa ndi Mulungu mwa Khristu ndipo ndiri kwathunthu wasachimwa.” “Kotero Yesu ine ndikubwera, ndipatseni kabukhu kakang’no.”

Moyo wathu ndi wotseguka kwa iro tsopano. Chabwino, vesi 9, Ndipo ndinapita kwa mngelo, (amene ndi Khristu) ndikunena kwa Iye, Ndipatseni kabukhu kakang’ono.” Tsopano taonani kulankhulana kwa awiri uku – kulumikizana kwathu ndi Ambuye, monga zinaliri mu masiku a Baibulo; kulankhula kwa Mngelo Wankulu, kwa Khristu, wodzozedwa, **“Ndipatseni kabukhu kakang’ono. Ndipo anati kwa ine, Tenga, ndikudya; kadzapanga mimba yako kuwawa, koma kadzakhala mkamwa mwako kozuna ngati uchi.”** Taonani kulankhulana kwa awiri uku! Abale ndi alongo, ngati inu muli fupa la fupa lake ndi nofu wa nofu wake; mamuna ndi mkazi wake amalankhulana. Yohane anati, “Ndipatseni kabukhu kakang’ono...” ndipo Khristu anati, “Tenga ndipo idya.” Iye akulankhula ndipo ndi chimene akuchita usiku uno, ndipo chonde wina usalingalire mwa thupi, ndi chimene Iye akuchita usiku uno, akulankhula, chifukwa Iye anaika utumiki usanu..., atumwi, aneneri, alaliki, abusa ndi aphunzitsi ndipo utumiki umenewo ndi umene Iye akuwugwiritsa ntchito kulankhula kwa Mkwatibwi Wake. Iye amalankhula kupyolera mwa iwo, kenako Iye amafulumizitsa chimenecho ku Mzimu wanu.

Kotero ine ndikukuuzani usiku uno, “Pitani mukatenge kabukhu kakang’ono, mfunseni Iye za iro.” Ndipo Iye akuti, “Tengani.” Iye wandilamulira ine kulankhula ichi..., “Tengani iro, idyani, lidzapanga mimba yanu kuwawa, koma lidzakoma mkamwa mwanu.” Haleluya, Paulo anati, “Iwo amalemekeza Khristu mwa ine.” Ena adzati, “Kumeneko ndikupanga munthu kukhala chinachake.” Ayi, inunso ndi gawo la icho. Iye anati, “Inu ndinu thupi la Khristu, mamembala a thupi la Khristu.” Iye anati, “Mwa Mzimu umodzi ife tabatizidwa mu thupi limodzi ndipo ndinu gawo la Khristu.” Kotero inu musaponye miyala Paulo chifukwa anati, “Iwo analemekeza Khristu mwa ine.” Ndipo ngati inu mutayang’ana pa izo ndi malingaliro a uzimu, inu mukhoza kulemekeza Khristu mwa ine pamene ine ndasandulika njira imene Iye akutsanuriramo Mau; ndipo ine ndikhoza kulemekeza Mulungu mwa inu, chifukwa tiri tonse gawo la Khristu, pamene tikudya kabukhu kakang’ono – “moyo weniweni wa Khristu.” Sizimatipangitsa inu kapena ine kukhala wopambana mzache, koma ndikukuuzani usiku uno, “Pitani mukatenge kabukhu kakang’ono, idyani. Inde kadzawawa.” Bukhulo ndi lotseguka, ndipo palibe chimene chiri chobisika kwa ife.

Inu mukudziwa mutati mubwerere ku masiku a Baibulo (ku Bukhu la Estere) panali mfumu uyu amene anatomiza anthu kukatenga atsikana. Pamene atsikana amenewa anafika pamodzi kwa nthawi yoyamba kudziyeretsa okha, panali mtsikana uyu dzina lake Estere, iye anangotenga zinthu zokhazo zimene zima funika ku kuyeretsa kwake. Pamene anafika pamaso pa mfumu, iye samayenera kulingalira za izo, iye samayenera kulimbana ndi lingaliro lake, iye samayenera kuitana gulu ndi kunena “Pali anamwali ambiri pano, ine nditenge uti?” Ayi, iye anasankha Estere, kotero Estere anapangidwira phwando ndipo anakwatiwa ndi mfumu. Anamwali ena aja anabwera nthawi yachiwiri, koma anaimitsidwa pa chipata – iwo sakanatha kudutsa chipata. Koma mkati mwa chipata chimenechi munali Estere ndi mfumu ali pa phwando. Limatchedwa phwando la Estere. Izi ndi zimene zikuchitika tsopano.

Pali anamwali ena, ndipo iwo akhoza kufika pa chipata. Iwo akhoza kunena, “Tipatseni ife mafuta anu ndi zinthu zina zochuluka zosiyanasiyana,” koma ndi Mfumu amene amasankha. Estere samafuna chirichonse chamaluwamaluwa, koma iye anangofunsa zokhazo zimene zinali zofunika pakuyeretsedwa kwake. Iye sakanatenga china chirichonse chimene chinali

chosayenera. Ine ndikukuuzani kuti ife tikuyenera kusiya chirichonse koma Mau a Mulungu, vumbulutso la Mau, Mzimu wa Mau...., ichi ndicho chiyeretso chathu. Mwa Khristu Yesu inu mwayeretsedwa.

Koma taonani; Iye anati, “Tenga bukhu!” Kodi mungaganize kuti ndikuchoka pa malo anga, (ndipo kumbukirani kuti mukuyenera kukhala gawo la izinso) inu ndinu thupi la Khristu, kodi mungaganize kuti ndikuchoka pa malo anga ngati ndi nditanena, “Wamphamvu zonse wandilamalira ine kuti ndikuuzeni inu kuti mupite mukatenge kabukhu kakang’ono, ndikotsegula.” Ndi chimene utumiki usanu uli, ndi kutsogolera, kuunikira ndi kutsogolera anthu a Mulungu monga Khristu akuwatsogolera iwo. Utumiki uwu kuno ku West Virginia wakhala ukundiiza, “Ife tikumverera kuti misonkhano iyi kuno ndi yoikika ndi Mulungu.” Inu mukuona utumiki kumbuyo uko kugwedeza mitu, kulankhula chomwecho mu umodzi ndi chimene ine ndikulankhula. Iwo anandiuza ine kuti amamverera ngati Mulungu alankhula kwa ife mu misonkhano iyi. Apo tiri! Mulungu walankhula mu misonkhano iyi.

Kupitiriza tsopano, taonani pamene Yohane amalankhula, “**Ndipo ndinatenga kabukhu kakang’ono,**” tsopano apo pali mfundo. Kodi inu mungatenge, mkati mwa mtima..., ndipo ine sindiitanira anthu kuguwa kapena kukhala ndi nthawi yokweza manja, chifukwa ichi mukuyenera kukhala inu. Kodi inu munganene ndi kuona mtima konse pamaso pa Mulungu kuti ndinatenga kabukhu kakang’ono? Amenewo ndi Mau, amenewo ndi Mau awa. Ine ndinatenga kabukhu kakang’ono. Ine ndikukhulupirira izi, ine ndikukhulupirira kuti izi ndi zinthu za Mulungu ndipo ndikukhulupirira mauthenga awa. Ine ndinalitenga iro – ndalitenga iro mkati mwanga. Yohane akuti, “Ine ndinapita kwa mngelo ndi kukanena, “Ndipatse kabukhu kakang’ono...” kenako iye anati, “Ine ndinatenga kabukhu kakang’ono.” Bukhu limene ndirotseguka ndi moyo wa Khristu umene ukusowa inu kwambiri kusiyana ndi dzulo. Kudzipereka kwanu kukuyenera kukwera pamwamba; ngakhale kuti chilungamo chanu sichingakhale chabwino (chifukwa chimakhala changwiro mwa Khristu) koma kudzipereka kwanu kukuyenera kukwera. Ndi chifukwa chake ndimapita ku madera onse a dziko kulalikira uthenga uwu. Ine ndimapita uko kuyesera kulalikira kuwala uku, chifukwa anati pita ndipo uchitengere ichi kwa athu onse, mafuko, ndi manenedwe.

Yohane anati, “Ine ndinatenga bukhu ndipo ndinalidya.” Mukuona misonkhano iyi yonse singachite chirichonse chabwino pokhapokha ife titadya, ndipo ngati titadya, inu ndi Mau mumasandulika chinthu chofanana. Inu mumatenga msinkhu wina wa chikhulupiriro, mumatenga msinkhu wina wa chiyembekezo, inu mumatenga msinkhu wina wa changu, inu mumatenga msinkhu wina wa chimwemwe, inu mumatenga msinkhu wina wa masomphenya ndipo inu mumatenga msinkhu wina wa chikhulupiriro ndipo m’dierekezi wagonja, chifukwa apo pali Khristu kubweranso ku dziko mu maonekedwe a mngelo kukupatsani inu zinthu zomwezo zimene Iye ali nazo. Inu ndinu wolowa pamodzi ndi Mulungu ndiponso wolowa ndi Khristu. Chinthu, (lonjezo) chimene Mulungu anamupatsa Iye, anachipereka kwa inu.

Mau anasamutsidwa, tsopano inu musaphonye ichi, Mau anasamutsidwa kuchoka mu dzanja la Khristu kubwera mu dzanja la utumiki, chifukwa ife tasandulika atumiki odalirika amene adzatenga Mau ndikuwagwira monga Paulo, monga Banaba, monga Timoteo, monga Tito amene Khristu anapereka Mau kwa iwo nanena, “Pitani kalalikireni uthenga.” Mau asamutsidwa. Mzimu womwewo wa Mau, mphamvu yomweyo ya Mau, ulamuliro wa Mau, Paulo anali nayo mu dzanja lake nthawi ina, chifukwa iye anali ndi Mau a Khristu. Pamene Khristu amayenda pano pa dziko asanapachikidwe, Iye analankhula chimene Atate ananena. Pamene Khristu anapita ndi kubwera pa tsiku la Pentekosite, mpingo unayamba kulankhula mau a Khristu ndipo nthawi zambiri zinali zosalembedwa mu zakuda kapena zoyera. Pali lemba limodzi limene ndimaligwiritsa ntchito nthawi zambiri ndipo ndikukhulupirira kuti inu simutopa nane kuligwiritsa ntchito, chifukwa iro ndi chitsanzo chomveka bwino. Ndi chimene Paulo analankhula zokhudza chiukitsiro ndi kusandulika kwa oyeramtima;

kumbukirani kuti zinali zisanalembedwe pena paliponse Paulo asanalankhule. Iye anati, “Iyi ndi njira imene zidzakhaliye, akufa mwa Khristu adzayamba kuuka,” tsopano taonani apa, chinachake chimene sichinalembedwepo mu Mau paliponse, inu simungapeze ngati chimenecho. Koma iye anati, “Akufa adzayamba kuuka, kenako ife amene tiri ndi moyo tidzasandulika mu kamphindi mu kuthwanima kwa diso ndi kutengedwa kukakumana naye Ambuye mu mulengalenga.” Kodi inu mungakhulupirire kuti panali anthu pamenepo atakhala ndi kukhulupirira zimenezo? Iwo sanalankhule, “Kodi iwe wazitenga kuti Paulo, tandiuzza pamene ziri?” **Ayi. Zinali mwa iye, ndi kumene zinali.** Anali Khristu mwa iye kulankhula, ndipo utumiki ukufika ku chimenechonso pamene tikulankhula. Mpingo sudzachoka pano mpakana tizindikire Khristu wamoyo pakati pathu. **Pamene zikutero, utumiki ngati gawo lachimuna la thupi limabweretsa Mau ku gawo la chikazi, ndipo zimabwera palimodzi..., zimenezo zimakupangitsani inu fupa la fupa Lake ndi nofu wa nofu Wake, Mzimu wa Mzimu Wake, mphamvu za mphamvu Zake, Mau a Mau Ake, inu mumasandulika m’modzi ndi Khristu.**

Kuwerenganso pang’ono apa, “*Ndipo ndinatenga kabukhu m’dzanja la mngelo, ndipo ndinakadya; ndipo kanali m’kamwa mwanga kozuna ngati uchi; ndipo pamene ndinakadya m’mimba mwanga mudawawa. Ndipo ananena nane, Uyenera iwe kuneneranso pa anthu ndi mitundu, ndi manenedwe, ndi mafumu ambiri.*”

Limodzi mwa ma ulendo athu ku Zambia, umodzi mwa misonkhano imene tinali nayo kumeneko..., m’bale wa ku Zambia amene sindinakumanepo naye, ndipo anasandulika omasulira wanga anali ndi maloto ife tisanafikeko. Iye anati, “Ine ndinaona munthu atakwera pa bulu wa golide, ndipo pamene amayenda panali zomvera m’makutu zimene zinayamba kutsikira kwa ife.” Iye anati, “Ine ndinayamba kuyang’ana ndipo nthambo zimene zinalumikiza zomvera m’makutuzo zinali zitakola kumwamba penapake; ndipo palibe aliyense amene amamva zimene munthu wokwera bulu wa golide uyu amalankhula popanda zomvera m’makutu zimene zinakola kumwamba.” Oh, Ine ndikukuuzani, ngati inu mutatenga vumbulutso la chimene zikutanthauza. Ndi kulalikira kwa vumbulutso lakuya la uneneri kumene sikungathe kumvedwa ndi kumvetsedwa mwa malingaliro a thupi. Zikuyenera kuperekedwa kwa inu kuchokera kumwamba. Kulankhula mwa uzimu, zomvera m’makutu zikutsika usiku uno; onetsetsani kuti mwatenga zanu.

Pali chitsanzo chimene ndikufuna kuti ndiwerenge ku Chivumbulutso chaputala 14, ndipo pali malemba ena apa amene amasiyanitsa kulalikira ndi kunenera. Kulalikira kwa utumiki usanu kumatchedwa kuneneraku Chivumbulutso chaputala 10:11; ndipo ndi utumiki usanu okha umene ukunenera. Mu malo ena kumatchedwa kulalikira; koma uku kumatchedwa kunenera mu vesi 11. Mau oti ‘*kunenera*’ kumakutengerani inu ku gawo la Uzimu ndipo wathupi samazimva. Ndi kulalikira, koma kulalikira kwa malankhulidwe a uneneri – monga Paulo, pamene iye anati, “Ife tidzasinthidwa mu kamphindi, mu kuthwanima kwa diso.” Koma tsopano pamene Ayuda 144, 000 adzabwera amene adzaitanidwa ndi aneneri awiri **kukulalikira** uthenga wosatha mu gawo lotsiriza la masabata 70 a Danieli, iwo adzapita kukachenjeza dziko (anthu a padziko) kuti asagwadire chirombo. Chimene ine ndikufuna kuti inu muone ndi chakuti Mau ndi abwino ndiponso omveka – sakugwiritsa ntchito Mau oti ‘*kunenera*’ apa, akugwiritsa ntchito “kulalikira.” Ndipo aliyense amene angathe kuwerenga akhoza kulalika, ngati angathe kudzuka ndi kumawerenga malemba. Koma ndi okhawo amene ali mu utumiki usanu amene akhoza kulankhula Mau a chinenero ndi kuwapatsa anthu chinachake chimene chikhoza mwantheradi kuyatsa mitima yawo, ndipo zidzakhala ngati moto mu mafupa awo umene udzawapangitsa iwo kudzuka ndi kunena, “Ine ndikukhulupirira tsopano.” Kotero ine ndikufuna kusiyanyitsa ichi.

Ndiloreni ine ndikuonetsereni kusiyana kwa “kulalikira” ndi “kunenera” monga ziriri apa. Chivumbulutso 14:1-3- “*Ndipo ndinapenya, taonani, Mwanawankhosayo alikuimirira pa phiri la Ziyoni, ndipo pamodzi ndi Iye zikwi zana mphambu makumi anai kudza anai kudza*

*anai, akukhala nalo dzina lache ndi dzina la Atate wache lolembedwa pamphumi pao. (Awa ndi Ayuda oitanidwa ndi aneneri awiri.) Ndipo ndinamva mau ochokera kumwamba ngati mkokomo wa madzi ambiri ndi ngati mau a bingu lalikulu; ndipo mau amene ndinawamva anakhala ngati a azeze akuyimba azeze awo; ndipo ayimba ngati nyimbo yatsopano ku mpando wachifumu, ndi pamaso pa zamoyo zinai, ndi akulu; ndipo palibe munthu anakhoza kuphunzira nyimboyi, koma zikwi zana mphambu makumi anai kudza anai, ogulidwa kuchokera kudziko.”*

Ine ndinamva chinachake chaching’ono chimene M’bale Jackson analankhula chimene ndikufuna kuonjezera apa ngati ndingathe. Ena a Mboni za Yehova anabwera kunyumba kwa M’bale Jackson ndi kulankhula, “M’bale, ife ndife 144, 000.” M’bale Jackson anati, “Kodi mungandiimbireko nyimbo imene palibe aliyense akuidziwa kupatula 144, 000?” Iwo anakwera galimoto yawo ndi kumapita! Palibe amene akuidziwa nyimbo imeneyo, koma 144, 000 okha!

Vesi 4-10 – *“Iwo ndiwo amene sanadetsedwa pamodzi ndi akazi; pakuti ali anamwali. (Iwo amatha kukwatira ndi kukhala ndi ana ochulukwa aliyense. Iwo sanadzetse ndi zipembezozo. Iwo sanadzetengere okha ziphunzitsa zachirendo; ndipo zimenezozo zinawapangitsa kukhala anamwali.) Iwo ndiwo amene anatsata Mwanawankhosa kulikonse amukako. Iwo anagulidwa mwa anthu, zipatso zoundukula kwa Mulungu ndi kwa Mwanawankhosa. Ndipo mkamwa mwawo simunapezeka bodza; (anali opanda chiphunzitsa chabodza) ali wopanda chilema. (Tsopano taonani) Ndipo ndinaona mngelo wina alikuuluka pakati pa mlengalenga, wakukhala nawo uthenga wabwino wosatha (ndipo siunalalikidwe mpakana pakati pa sabata la 70 la Danieli). (Taonani) **kukulalikira** (taonani mau amenewo “kulalikira.” Kodi kulalikira ndi chiyani? Kudzuka ndi kuyamba kupfuula. Kutenga Mau ndi kupfuula kuchokera ku Mau a Mulungu. Ine ndikhoza kutenga zinthu zolimba kuchokera mu Concordance ndi kutengamo malemba ochulukwa ndi kuima pano kulalikira. Koma taonani 144, 000, iwo anali oti alalikire, osati kuti anenere. Awa ndi Ayuda otulutsidwa, ndipo sapangitsa anthu kupulumuka ndi kubadwa mwatsopano, koma ndi ochenjeza anthu kuti asalambire kachitidwe ka dziko, chifukwa mileniamu yatsala pang’ono kuchitika.) Tsopano taonani – wakukhala nawo uthenga wabwino wosatha aulalikire kwa iwo akukhala padziko, ndi kwa mtundu uliwonse ndi pfuko ndi manenedwe ndi anthu, (chomwecho momwe zinaliri ndi Mkwatibwi, mwa kuti zinali za dziko lonse) Kulankhula ndi mau akulu, (Ndipo apa pali chimene adzalalikire kwa iwo. Iwo sanadye kabukhu kakang’ono. Ichi ndi chimene akunena kwa iwo, “Opani Mulungu, mpatseni ulemere; pakuti yafika nthawi ya chiweruziro chake; ndipo mlambireni Iye amene analenga mwamba ndi mtunda ndi nyanja ndi akasupe amadzi. Ndipo anatsata mngelo wina mnzache ndi kunena, Wagwa wagwa Babulo waukulu umene unamwetsako mitundu yonse ku vinyo wa mkwiyo wa chigololo chake. (144, 000 awa adzamuchitisa manyazi Babulo.) Ndipo mngelo wachitatu (Padzakhala magawo atatu a izo.) Ndipo anawatsata mngelo wina wachitatu nanena, Ngati wina alambira chirombocho, ndi fano lache, nalandira lemba pamphumi pache, kapena pa dzanja lache, iye adzamwako ku vinyo wa mkwiyo wa Mulungu...”*

Apa pali chimene ndikufuna inu kuti muone – “awa akulalikira;” iwo a ku Chivumbulutso, chaputala 10:8-11 akunenera. Kunenera kuli ndi tanthauzo lakuti ndi mwa vumbulutso lokha mukhoza kumva izo. Pokhapokha mutakoleka zomvera m’makutu zanu kumwamba inu mukhoza kumva izo; koma mukhoza kumva kulalikira. Inu mukhoza kumva Uthenga Wosatha umene 144, 000 akulalikira. Padzakhala anthu amene adzapita ku mileniamu ndipo iwo sanalambire chirombo kapena fano lake. Kodi mukutha kusiyantsa? Ndi chimene takhala tikuchita nthawi zambiri; ife takhala tikulalikira. Koma tsopano Mulungu watsegula kabukhu kakang’ono ndikutipatsa ife ndi kunena, “Pitani kanenereni.” Kwezani izo ku muyeso wina kudutsa ulaliki ndipo ulaliki udzakhala uthenga wauneneri. Tengani izi kwa anthu onse, mafuko, ndi manenedwe. Ine sindimadziwa m’mene ichi chingachitikire. Ndi

zovuta kuzichita mwa kupanga maulendo, koma kupyolera pa internet iwo akhoza kumva izo kulikonse, dziko liri lonse nthawi iriyonse, kulikonse kumene kuli computer ndi tefoni. Akhoza kukopera izo paliponse. Uthenga ukupita pa dziko lose lapansi pamene tikulankhula, kwa anthu onse, mafuko ndi manenedwe, ndi mafumu (kapena maufumu).

Tsopano Khristu wabwera ndipo watipatsa ife kabukhu kakang'ono. Tsopano kukupatsani inu kabukhu kakang'ono ndi chimodzimodzi kukupatsani inu zomvera m'makutu. Kupereka kabukhu kakang'ono kuli chimodzimodzi pamene Khristu anatsika kumwamba, Iye anamanga ndende undende ndipo anapereka mphatso kwa amuna..., ndipo amuna amewo analalikira Mau a Mulungu ndipo thupi lonse linasandulika chimene iwo amalalikira.

Kotero, apa mu masiku otsiriza, pamene Iye akuti, "Pita katenge kabukhu kakang'ono ndi kudya," ndi chimodzimodzi kupereka mphatso kwa amuna. Iye anapereka utumiki usanu choyamba, ndipo iwo ananenera; ndiye kenako mpingo wonse unayamba kunenera; osati akazi kudzuka ndi kuyamba kulalikira uthenga kutsogolera mpingo; koma alankhula za izo. Iwo amalankhula za Yesu. Iwo amafuna kulankhula za zinthu za Mulungu. Iwo amachitira umboni zinthu za Mulungu. Iwo amatenga vumbulutso la izo. Aliyense akulankhula za chinthu chofanana, kukhulupirira chinthu chofanana. Aliyense wakwezedwa pamwamba. Aliyense akuyenda ndi Mulungu. Chikhulupiriro cha aliyense chikukwera, ndipo aliyense akukhulupirira Mulungu ndipo amapita ku chinthu chofanana; chifukwa pamene tilalikira Mau, ndipo inu muwalandira ndi kuwakhulupirira iwo, inu mumasandulika gawo la Mau. Ameneyo ndiye Mkwatibwi, pamene tonse tikudya kabukhu kakang'ono..., monga Malaki, chaputala 3:16 – 17 akunena, ***"Pamenepo iwo akuopa Yehova analankhulana wina ndi mnzache; ndipo Yehova anawachera khutu namva, ndi bukhu la chikumbutso linalembedwa pa maso pache, la kwa iwo akuopa Yehova, nakumbukira dzina lache. Ndipo iwo adzakhala anga anga, ati Yehova wa makamu, tsiku ndidzaikalo, ndipo ndidzawaleka monga munthu aleka mwana wache womtumikira."***

Tsopano, kabukhu kakang'ono (Mau olankhulidwa, Moyo wa Khristu) unali wotsegulidwa ndi opezeka ku mpingo wa pa chiyambi. Unasindikizidwa mu 96 A.D. Mau a ulamuliro analamulira Yohane kusindikiza ndipo anati "Lorani tirigu ndi namsongole zikulire palimodzi." Koma pamene mu masiku otsiriza Mulungu analamulira munthu, M'bale William Branham, amene anali wofanana ndi aneneri aku Chipangano Chakale; ndipo iye analalikira zisindikizo zisanu ndi ziwiri pamene Mwanawankhoza anamasula izo kumwamba ndi kuzitumiza izo kwa mneneri Wake mwa angelo asanu ndi awiri a ku bukhu la Chivumbulutso, chaputala 10:3 – 4. Ndipo tsopano apa pakubwera Khristu ndipo bukhu ndi lotsegula tsopano, likutiika penipeni pakati pa chimene Mulungu akuchita – Khristu pakati pa ife chiyembekezo cha ulemelero, kudya kabukhu kakang'ono, ndi uthenga wauneneri. Okhawa amene angatenge uthenga wa uneneri umenewu ndi mamembala a mu utumiki usanu..., chifukwa pamene Iye anakwera kupita kumwamba Iye anapereka mphatso kwa amuna. Iye anaika utumiki umenewu mu Mau ndipo umayenera kuyamba kugwira ntchito mu tsiku iri lotsiriza kufikitsa Mkwatibwi ku chidzalo cha Khristu. Tsopano ife tiri nawo utumiki usanu ndipo Iye akulamulira mau kwa ife. Ine ndikufuna ndikufunsemi inu, kodi mukuganiza kuti mau awa akubwera bwanji? Akubwera kuchokera ku utumiki wa munthawi ino, umene ndi Aefeso, chaputala 4:11; ndipo izi zimakulamulirani inu kutenga kabukhu kakang'ono. Inu mwalamulidwa kudya kabukhu kakang'ono. Inu mwalamulidwa kusandulika chirichonse chimene mpingo woyamba unali ndi mochuluka. Inu mwalamuliridwa kugonjetsa woipayo nthawi iriyonse. Inu mwalamuliridwa kufunsa chilungamo cha Yesu Khristu. Iye anasandulika tchimo chifukwa cha inu kuti inu musandulike chilungamo Chake; ndipo mwalamulidwa kufunsa icho, kuchitenga ndi kuchiika pa inu.

Ambuye akudalitseni. Tiyeni tipemphere. *Atate, mu dzina la Yesu, Ambuye ife tikupereka Mau awa kwa inu, uthenga uwu. Ambuye, ine ndikuthokoza inu chifukwa cha anthu awa amene abwera njira iyi misonkhano itatu iyi. Ambuye, ine ndikudziwa kuti mu gawo la*

umunthu ife tikhoza kunena, “Ine sindinaone moto.” Ife tikhoza kunena “Ine sindinaone aliyense mwambamu.” Ife tikhoza kunena, “Ine sindinamve aliyense akulankhula mu malirime.” Ife tikhoza kunena sindidawone anthu akugwedezeka. Ine sindinaone aliyense akuchita mwauzimu mu njira ya thupi.” Ambuye, koma ine ndaona anthu akulandira Mau. Koma Ambuye, lorani aliyense pano akhale nako kuzindikira kwakukulu kuti china chake chapangika, chinachake chachitika. Inu mwalandira ndipo inu mwachita chinachake, ndipo ife tiri gawo la icho Ambuye. Ndipo Mau akulu a ulamuliro, mau omwewo amene analankhula kwa Yohane, ndipo iye anali munthu wokalamba, iwo amaganiza kuti iye anali wokalamba kwambiri. Aroma sakanatha ngakhale kumupha munthu wokalambayo; iwo anamva chisoni ndipo anamuika iye pa chisumbu kuti amwalire pomweko. Iye anali wokalamba kwambiri kuti agwire ntchito, iwo amaganiza choncho. Koma Ambuye, inu munabwera ndikulankhula kupyolera mwa iye ndi kwa iye, ndipo panali mau aulamuliro akulu amene anamupatsa iye zisindikizo ndi zonse za izo ndi kumuonetsera iye; ndipo amafuna kulemba chimene chidzakhale, koma Ambuye, inu munamulamulira kuti asindikize bukhu ndi kulisiya losindikizidwa kufikira mngelo wachisanu ndi chiwiri anabwera ndi kutsiriza zinsinsi zonse zimene zinali zolingana ndi zimenezo. Ndiye Ambuye inu munabweranso, tsopano, yemweyo amene analankhula ndi Paulo, yemweyo amene analankhula ndi Anania, yemweyo amene analankhula ndi Petro... Ambuye, bukhu limenelo ndi lotseguka kwa ife tsopano, ndipo Inu kachiwirinso mwalamulira. Mulungu, tithandizeni kuti tisadzinyoze chifukwa cha kudzichepetsa kwake. Ndi zopheka moti tikhoza kulakwitsa. Ife tikhoza kunena, “Ine ndimagaganiza kuti akanachita ichi; ine ndimagaganiza akanachita icho.” Ambuye, lorani aliyense adziwe kuti inu mwabwera pakati pathu ndipo mwalamulira chinachake mwa mau akulu a ulamuliro kuchokera kumwamba amene abwera. Ndipo Ambuye, ife tikuthokoza kuti mwasankha malo ano kuno ku West Virginia kutumiza mau awa, ndipo kuchokera pano apita pa thambo lonse. Mulungu, Ine ndikupemphera tsopano kuti mitima ya aliyense idzakwezedwa, **ndipo kuti aliyense adzazindikira Ndamva mau a ulamuliro a Wamphamvu zonse akunena**, “Pita ukatenge kabukhu kakang’ono; Khala chimene mpingo wapachiyambi unali; palibe malire oikidwa pa icho; zonse ndi zotheka kwa onse amene akhulupirira.” Ambuye, ine ndikupemphera kuti inu mudzadzaza chotengera chirichonse ndi chimwemwe cha Ambuye, ndi mphamvu ya Mulungu, ndi vumbulutso la Mulungu, kuti tikapitirire. Ndipo Ambuye, pamene tikupita njira yathu, ngakhale mawa, zipitirire kukhazikika mkati, zikhale mu malingaliro a wina aliyense, ndipo iwo akhale mu chikhulupiriro chomwecho. Pamene akuonjezera, Ambuye, ine ndikudziwa kuti inu mudzaonjezera. Ndipo iwo azindikire ichi kuti zinalonjezedwa ndi Wamphamvu zonse. Tikupempha izi mu dzina la Yesu kuti mudalitse ndi kuthandiza anthu. Amen.